

KODI MASOMPHENYA

NDI CHIANI?

 Zikomo inu, mochuluka kwambiri. Tiyeni ife tipemphere.

² Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha ubwino Wanu wonse kwa ife. Mulungu, ife tikungomverera osayenera, ndi poyang'ana pa omvetsera awa lero ndi kuwona keke ya tsiku lobadwa iyi ili apa. Ine ndikupepesa, Atate. Inu mundikhululukire ine. Ine sindingakhoze basi kuyankhula. Koma ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mwanjira yina, mwanjira yina, kuti mtsinje wa chikondi Chaumulungu uwu ungomuthandiza aliyense. Adalitseni anthu awa omwe achita chinthu chachikulu ichi, Atate. Ine ndikungopempha kuti madalitso Anu akhale ndi ife, mokula kwambiri, lero, mpaka nyumba yonse yisefukire ndi Ulemerero Wanu. Ndi—ndipo poganiza za nthawi yomweyi poyang'ana pa anthu ogontha ndi osayankhula awo akudutsa, akupita kumbali yina. O, ine ndikupemphera, Mulungu, mwanjirayina, muchite chinachake mwanjira yaikulu kwa ife lero. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

³ Madalitso a Mulungu atakhala pa Buckman. Ine ndikungopemphera kuti Mulungu akudalitseni inu, abwenzi anga okonedwa. Icho ndi chinthu chokongola kwambiri. Ine ndikulingalira...Kodi inu mwachisonyeza icho kwa gulu? Kodi atero [M'bale ati, "Inde."—Mkonzi.] Eya. Kodi icho si chokongola? [Osonkhana ati, "Inde."] Ine ndikufuna kuti nditenge nthawi iyi kuti ndikuthokozeni inu. Palibe njira mu dziko yomwe ine ndingakhoze konse kukulipirani aliyense wa inu chifukwa cha madalitso anu achifundo. Ndipo ine ndinazindikira mphatso zomwe zinaperekedwa kwa ine, ndiponso mphatso zazing'ono mu ma enivelopu, ndi makadi ndi zinthu. Zodabwitsa! Zikungondipangitsa ine kumverera ngati ine ndikufuna nditapanga dongosolo, lodzabwerera chaka chikudzachi pa tsiku langa lobadwa. [Osonkhana akuwomba manja awo.] Zikomo inu, mwachifundo. Mai! Izo ndi zodabwitsa. Ine ndimayang'ana pozungulira; ine sindimadziwa chomwe izo zinali. Ndipo izo zedi ndi zokongola, ndi mphatso zanu zonse.

⁴ Chiripo chinthu chimodzi chokha chimene ine ndingakhoze kunena. Ndipo ichi sichiri ndendende...Chabwino, ndiko kunena, ndi pemphero, "Mulungu akudalitseni inu." Ndipo ngati ine sindidzakhoza konse...ndipo Mulungu akapanda kundilola ine kuti ndizichite izo mu moyo uno, ku—kuti ndisonyeze mayamikiro anga chifukwa cha mphatso zonse izi zochokera

kwa aliyense. Ngakhale msungwana wamng'ono anali ndi enivelopu yaing'ono mmenemo, ndipo icho chinali chakhumi chake, cha pafupi masenti eyiti, ine ndikuganiza iyo inali. Iye anaitumiza iyo kwa ine ngati chopereka cha tsiku lobadwa, chakhumi chake. Kuyambira pa icho, mpaka ku zopereka zazikulu izi kuno, o, Mulungu akulipireni inu molemera, abale anga okonedwa ndi alongo. Ine basi. . . Ine sindimaganiza kuti inu mumaganiza kwenikweni mochuluka chomwecho za ine. Ine ndinali kwenikweni. Ine ndiri kuziyamikira izo.

⁵ Lero, ndi—ndi, ife tinazitenga izo kukhala kuyankhulana kwa mtima ndi mtima, ine ndikukhulupirira, lero. Basi, mmalo moti ndilalikire uko kunali kungoyankhula ndipo mwinauwake kufotokoza zinthu zina zomwe zingawoneke zachinsinsi kwambiri kwa inu mu misonkhano. Zikukhala ngati zobanikitsa. Basi, ine sindimayembekezera tsiku lobadwa lina lero.

⁶ Ndipo pakungobwera pa khomo, ndinakomana naye mzanga wabwino kuno, Art Wilson. Ine ndikuganiza amuna amalonda Achikristu onse akumudziwa iye. Kwanu—kwanu ndi ku Oregon, si choncho? Kapena. . . [M'bale Wilson ati, “Reno, Nevada.”—Mkonzi.] Reno, Nevada. M'bale Art Wilson, kumanja kwanga.

⁷ Bambo winayo ndi Bambo Woods. Bambo Banks Woods, ndi bwenzi wanga ndi woyandikana naye. Bambo Woods akhala akupita ndi ine. Ndipo ambiri a anthu inu mukuwadziwa iwo, pakugulitsa mabuku mu msonkhano. Bamboyo wakhala wazomangamanga wochitabwino kwambiri. Ndipo tsiku lina, pamene ine ndinali mu Louisville, Kentucky, tiri ndi msonkhano; iyemwini pokhala wa Mboni za Yehova, akazi awo pokhala a Methodist. Iwo anali atamva za msonkhano, kotero iwo anangoyendetsa nabwera kuti adzaone momwe zinaliri zoon.

⁸ Pa usiku umenewo, uko kunali msungwana yemwe anawumitsidwa, anali atagona kwa miyezi ingapo, samakhoza ngakhale kuti asunthe polumikizira paliponse, kuchokera mchiuno mwake mpaka mmusi. Dona wamng'ono wa pafupi, o, abiti wa pafupi usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu, anauka apo pomwe kuchokera pa machira, pamene anali kubweretsedwa ku nsanja, anayenda pamalo ponsepo. Tsiku lotsatira, anangopitirira. Anabwerera ku sukulu mu masiku pang'ono. Alibwino bwino, apobe. Ndi zinthu zambiri Ambuye anazichita.

⁹ Kotero Bambo Woods, pokhala ali ndi chinachake choti achite, nyumba yoti ayitsirizitse, kapena chinachake chomwe iwo anali kuchichita, iwo ankayenera kuti afulumire ndi kukazichita izo; anapita ku Houston, Texas, ku msonkhano wanga wotsatira. Uko, iwo anali ataima mu chipinda usiku umenewo pamene Mngelo wa Ambuye anawonekera, ndipo

makamera anagwira chithunzi cha Mngeloyo, momwe, chithunzicho inu mwachiwona, nokha, muno.

¹⁰ Ndiye, iwo anali ndi chimodzi cha zosankha zawo. Iwo anali ndi mnyamata wolumala, ndipo mwendo wake unali utakokekera pansi pake. Ndiyeno Bambo Woods, pamene ine ndinabwererako... Ine ndinali nditapita kutsidya kwa nyanja, ndi mpaka ku Sweden; ndi kubwererako. Ndiyeno iwo anadzaika hema uko, ine ndikukhulupirira uko kunali ku, Cleveland kapena... Cleveland, Ohio. Ndipo Bambo Woods, apobe, ndithudi mu unyinjira, ankangotsatira konseko, monga a ambiri inu mukanalilo lero, koma anatsimikiza kuti atsalira mpaka iwo utatha. Ndiyo njira yake, njira yochitira izo. Ndipo iye anaika pambali ntchito yake ndipo anamubweretsa mnyamatayo uko ku Cleveland.

¹¹ Atatha mausiku pang'ono, izo zinali mu msonkhano. Ndithudi, ine sindimazikumbukira; mwa tepi yokha basi. Iwo anali atakhala mmbuyo mu hema, mmbuyo momwe, iwo ndi akazi awo. Ndipo Mzimu Woyera unabwera pansi ndipo unati, "Dona wakhala kumbuyo uko ali ndi mwamuna wake, wazomangamanga," unati, "iye mwiniwake ali ndi chotupa. Ndipo mnyamata wake ndi wolumala. Koma, PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Wachiritsidwa.'" Anamudzutsa mnyamatayo. Iye ndi mnyamata, wabwino, wa mwendo wowongoka, kuyambira ora ilo lomwe, wolunga basi monga mnyamata aliyense angakhoze kukhalira.

¹² Bambo Woods anasiya zomangamanga; akulova ndi ine. [Osonkhana akuwomba mmanja mwawo—Mkonzi.] Koterolo, mnyamata wawo ndi mnyamata wanga ndi abwenzi kwambiri, limodzi. Ndipo iye ndi wolunga basi ndi wochira monga mnyamata aliyense, akuyembekezera kuti azipita ku nkondo posachedwa. Choterolo, Ambuye ndi abwino. Si choncho Iye? ["Ameni."] Iye ndi wodzaza chifundo. Ndipo kuchuluka kwa zinthu zazikulu zomwe Iye wazichita pakati pathu!

¹³ Tsopano, lero, tsopano, usikuuno, ine ndikuganiza, pokhala kuti... Iye tiyamba molawirira pang'ono. Ine ndiyenera kuti ndikakhale mu Louisville, Kentucky, mwa chigwirizano mmawa, pa eyiti koloko, ndipo ndiyenera kuti ndiyendetse njira yonse mpaka uko, usikuuno, komwe kuli kuyendetsa kwa pafupi maora-eyiti-kapena teni. Choterolo, ife tikafika uko basi pafupi mu nthawi yoti tikafike ku chigwirizano. Iye tinyamuka molunjika basi kuchokera kuno, wa... ku Louisville, ndi pa galimoto. Ndiyeno ife tikulinga kuti tiyambe misonkhano molawirira pang'ono basi, usikuuno. Ndipo ife tiyamikira kubwera kwanu, molawirira pang'ono basi, ngati inu mungatero. Iwo anandiuza ine kuti ndingadzakhale pa nsanja...

14 [M'bale Joseph Mattsson-Boze ati, “Makadi azidzaperekedwa pa sikisi koloko.”—Mkonzi.] Makadi azidzaperekedwa pa sikisi koloko, M'bale Joseph watero. Ndipo ife tinali basi. . .

15 Ankhondo mwina amutenga Billy posachedwa kwambiri, chotero Bambo Woods akupereka makadi apemphero, ndipo Billy akuwaphunzitsa iwo. Ine ndinati, “Zikuyenda bwanji, Bambo Woods?”

16 Iwo anati, “Nnena!” Iwo anati, “Ziribwino, koma,” anati, “Ine ndinali ndi makadi awiri okha ndipo ndinali ndi anthu sikisi amawafuna iwo.” Ndizo. . .Iye anati, “Inu mumatani zikakhala chomwecho?”

Ine ndinati, “Basi zomwe inu munachitazo.” Ine ndinati, “Chabwino, iye. . .”

17 Ndipo usiku watha, pamene iye anali atakondwa kwambiri, iye anati, powawona anthu omwe—omwe iye anali atawapatsa makadi, ataima pa nsanja, ndipo Mulungu akuwachiza iwo ndi kuwapangitsa iwo kuchira. Ndipo iye anali wokondwa kwambiri nazo!

18 Tsopano, usikuuno, ndi woti aperekedwa pa sikisi, chifukwa ine ndikuganiza ine ndiyenera kuti ndidzakhale pa nsanja pa kotala pasiti eyiti. Ine ndikukhulupirira ndiko kulondola. Ndiyeno, chotero ife tikhoza kubalalika molawirira pang’ono, pa chifukwa cha kuyendetsa kwakutali, kotopetsa usikuuno.

19 Chotero, zikomo inu, chifukwa chobwera, madzulo ano. Ndipo pa madzulo amphepo, ozizira awa, ndipo komabe inu munabwera. Izo zikusonyeza kuti inu simunabwere kuti mudzaonedwe. Inu mwabwera chifukwa cha zabwino zomwe inu mungazipeze kuchokera mu msonkhanowu, kuchokera kwa Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Iye akudalitseni inu, mochuluka.

20 Tsopano, makamaka, izo sizikutanthauza kuti anthu ayenera kudzakhala ali pano pofika sikisi koloko; inu nokha omwe mukufuna makadi a pemphero.

21 Ndipo tsopano Ambuye atawonjezera madalitso Ake kwa onse osonkhana athu palimodzi. Ndipo ine—ine ndikuyembekeza kuti tsiku lina, Ambuye akalola, posachedwapa ndidzabwerera mu Chicago kachiwiri, ndi kudzawatumikira Ambuye.

22 Baibulo linanena apa:

Ngati pali wina yemwe ali wauzimu kapena mneneri pakati pa inu, Ine YEHOVA ndizidzidziwitsa ndekha kwa iye mu masomphenya, . . .

23 Ambuye atawonjezera madalitso Awo kwa Mawu Awo. Tsopano, mwa kuyankhulana kwa mtima-ndi-mtima basi. Ine ndati. . .

24 Joseph sakudziwa izi. Koma ine ndikuti ndingomupempha iye ngati iye angati basi, nthawi iliyonse yomwe iye angafune kuti, andidukize ine kuyankhula, ndi kunenapo chirichonse. Ife tinali nako kuyankhulana pa zina zonga izi, mmawa uno, pa walesi. Kodi inu nonse munaimva programuyo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

25 Ndi—ndipo chotero ndiye, l—lero, ine ndinaganiza, mwina mongokhala ngati ndigwire—kumverera kwa anthu, chotero kuti inu mukhoze kuwona izo, kugwira ntchito kwa zauzimu. Ndi kungopereka kuyankhulana kwa mtima ndi mtima kwa wina ndi mzake, kukulolani inu kuti mulowe mkati mwa Izi, basi utali womwe ine ndingakhoze kupitira. Ndipo ine sindinayambe konse. . . Zochuluka za zinthu izi zomwe ine ndiri nazo pa mtima wanga kuti ndizinene, ine sindinayambe ndazinenapo kwa omvetsera kale, mu moyo wanga. Chotero Iye atawonjezera madalitso Ake ku zomwe ife titi tinene.

26 Chinthu choyamba chimene ife tikufuna kuti tichikambe ndi: *Kodi Masomphenya Ndi Chiani?* Kodi iwo angakhale ali chiani? Ena, anthu ochuluka kwambiri. . .

27 Ine sindiri kunena, monga M'bale wathu Billy Graham ananena, “Poyankha onditsutsa anga.” Ine ndiri wothokoza kwambiri kuti ine ndiri nawo onditsutsa pang’ono kwambiri. Pafupi aliyense. . .

28 Ena a iwo omwe sanayambe akhalapo ku msonkhano, iwo akhoza kunena, “O, chabwino, palibe kanthu kwa izo.” Koma kamodzi mu msonkhano, izo pafupi ndithu zimawakhazikitsa iwo nthawizonse, pamene Yesu awugwira mtima wawo, ndipo iwo akawona ndiye kuti ndi—kuti ndi zoonza.

29 Masomphenya ali—ali basi. . . Anthu ambiri amandifunsa ine, “M'bale Branham, kodi ndi chogwirika chimene inu mumayang’anapo? Kapena, kodi chimangokhala chongokondweretsa mu malingaliro? Kapena, nchiani icho?” Ayi. Chimakhala chogwirika. Chimakhala chenicheni basi monga ine ndiri kuyang’anira pakali pano.

30 Ndipo tsopano, momwe izo zimachitikira, izo zimachitika mwa chisomo chapayekha cha Mulungu. Ndipo pamene ndinali khanda chabe, pamene ine ndinabadwa koyamba, mayi anga amandiuza ine kuti Kuwala uku kunadza ndi kudzapachikika pa kama wamng’ono pomwe ine ndinabadwirapo. Ndiyeno, kuyambira pomwe ine ndingakhoze kukumbukira, zinthu izo zakhala zikuchitika patsogolo panga.

31 Basi, iwo amangotseguka. Zimangowoneka ngati palibe njira yomwe ine ndingakhoze kuzifotokozerza izo kwenikweni; koma, basi kuti ndipeze zopambana zomwe ine ndingakhoze: ndimangodziperekera kwa Mzimu Woyera. Ndipo iwo umangoyambitsa, ndipo apo iwo amakhala ali patsogolo pa iwe. Iwe umadziwa kuti iwe wayima pano, ndipo komabe iwe uli

zaka makumi anai mmbuyo mu moyo wa winawake, kumawona zomwe iwo akupanga. Ndiyeno, chinthu chokha chimene ine ndimanena, ndi chokhacho chomwe ine ndikuchiyang'anacho.

³² Ndiyeno pamene ine ndikhala ngati ndabwerera kwa inemwini, ine ndimazindikira kuti ndinanena chinachake, koma nthawi zambiri ine sindimadziwa zomwe ine ndinanena. Ndipo momwe ine ndimazipezera izo, ndi anyamata awa, awo akhala mmusi umu, matepi rekoda awa, iwo amasewera mobwereza izo kwa ine. Ndipo ndi momwe ine ndimazipezera izo. Kotero, izo sizimakhala mwa inendekha, konse.

³³ Ndiyeno izo—izo zimaperekedwa k—kwa cholinga chimodzi. Tsopano, ine ndikuganiza, ndipo ine ndikunena izi kuchokera mu mtima mwanga, kuti njira yaikulu kwambiri ndi yapamwamba yomwe ilipo yoti Mulungu azipereka Uthenga Wake kwa anthu Ake, ndiyo kuti anthu azikhulupirira Mawu Ake. Ndiko kulondola. Ndiyo njira yapamwamba kwambiri. Kulalikira Uthenga ndi njira yapamwamba kwambiri. Ndiye, ngati inu mungazindikire, Baibulo limaziyika izo mwa njira imeneyo. “Choyamba atumwi, kachiwiri mneneri,” ndi ena otero, ndiye mpaka mmusi, mpaka mmusi, ndiye mpaka ku mphatso zauzimu zisanu ndi zinai zogwira ntchito mu thupi wamba lirilonse.

³⁴ Tsopano, misonkhano yanga mu Amereka sinakhale yabwino kwambiri monga momwe iyo ikanati izikhalira, mu Amereka. Misonkhano yanga ikumakhala yamphamvu kwambiri, kwa Ambuye, kutsidya kwanyanja. Iwo amadza kwa iyo mwabwino. Tsopano, ine sindikudziwa chifukwa chake. Tsopano, ine sindiri kuyankhula za inu anthu. Ayi. Ine ndikuyankhula za anthu wamba, onani, konse kozungulira, monga Chicago, mwa yense, ife tingati; ka—kapena, Durban, South Afrika, mwa yense, mukuona, chinachake monga choncho; kapena, Mzinda wa Mexico, mwa wonse. Chabwino, iwo amavomereza kwa iwo, magawo eyite pa zana kuposa momwe iwo angachitire mu Amereka.

³⁵ Tsopano, chimene Achimereka amavomerezako mwabwino, ku misonkhano ya machiritso, mwa kulingalira kwanga, ndi, eedi, ya M'bale Oral Roberts. Tsopano, M'bale Oral Roberts ndi woyankhula wamphamvu, mlaliki weniweni, ndiponso m'bale wabwino wowopa—Mulungu, m'bale wathu, Oral Roberts; ndi bwenzi wa pa mtima wanga, m'bale wokondeka. Ndipo ine ndiri nako kulemekeza kwakukulu, kwakuya kwa M'bale Roberts. Ndipo Ambuye ali ndi iye ndipo akumudalitsa iye, mopambana, ndi misonkhano yake muno mu Amereka. Iye . . .

³⁶ Ife tonse tikhoza kupita mu mzinda, ndipo iye nkukonza msonkhano wake, ndipo ine nkukonza msonkhano wanga. Omvetsera ake angawameze anga, mochulukitsa kwambiri, ndi kulengeza kochepe kokha, chifukwa utumiki wake uli nako

kukhudza kwakukulu muno mu Amereka, chifukwa iye ndi woyankhula wo—wo—wokopa chotero. Iye ndi. . . Ndipo iye ali nayo—njira. Iye ndi wanzeru ndi wophunzira, ndipo amalidziwa Baibulo. Ndipo iye akhoza kulipereka ilo mwa njira yakuti anthu ophunzira amamvetsera kwa izo, chifukwa ndizo ziri pa muyezo womwe iwo—iwo ali kukhala.

³⁷ Koma titengeni ife, pamene ife tinapita ku Afrika, chabwino, uko kunalibe kufanizitsa, konse. Mwaona? Ndipo anthu omwe ali osaphunzira, ena otero, amafunafuna zauzimu, chifukwa iwo alibe izi, maphunziro ndi. . . kuphunzitsidwa kwausikolala monga anthu awa kuno. Kotero ndiye. . . Ndicho chinthu chomwe Ambuye atipatsa, kuti tizipindulira nacho anthu.

³⁸ Tsopano, ine sindikutanthauza kunena kuti. . . Ambiri ophunzira, anzeru, othyathyalika, ena a pamwamba, ngakhale mafumu, amphamvu, mafumu, ndithudi, iwo amazikhulupirira izi ndipo amazilandira izo.

³⁹ Koma mwa kuchita kwawamba, mipingo yathu ya Chimereka, yakhala ili nthawi yaitali kuchokera pamene ife tinakhala nacho chitsitsimutso, kuyambira mmbuyo kutali mu m’badwo wa Wesile. Timibadwo takaletu tinazirara. Pamene, anthu achi Wesile anali kumakankhidwira kunja ndi kumatchedwa “oyera-odzigudubuza” ndi “odzigwedeza,” chifukwa iwo ankagwedeza mutu wawo, ndi—ndi kudzigonetsa. . . pa nsanja ndiponse pozungulira, mu timipita. Iwo ankatsanulira madzi pa iwo ndi kumawakupizira iwo, pamene Mzimu Woyera unakhala pa iwo. Tsopano, tsiku limenelo linazirara, nthawi yaitali kale.

⁴⁰ Ife tonse takhazikika pano, o, Achiorthodox kwambiri. Koma ndicho chifukwa iwo sangakhoze. Anthu lero akuphunzitsidwa, chabwino, w—woyankhula yemwe angakhoze kuzipereka izo mwa—mwanjira yaukatswiri. Chabwino, ndizo zabwino basi. Izo ndi zabwino basi ndi zokoma. Ndipo bola ngati inu mwalandira Khristu, ndicho—ndicho chinthu chachikulu, basi bola ngati inu mwamulandira Khristu.

⁴¹ Tsopano, ife tikuzindikira M’bale wathu Roberts. Inu munamvera purogramu yake mmawa uno, mwinamwake. Ndipo ine ndinawerenga nkhani mu pepala, ndipo ndinazimva izo mwandekha. Kuyambira momwe kuti. . . Ndipo mpaka mu Australia, chinthu choyipa chomwe chiri, iwo akuchemerera, kumamutcha iye “wonamizira” ndi chirichonse, ndi kumuthamangitsa iye uko monga choncho. Kumene, mwinamwake. . . utumiki wa mtundu uwu ukanatontholeta chinthu choterocho, pakali pano. Mwaona? Mwaona? Izo zikanakhala mosiyana. Ndipo, koma, M’bale Roberts, apobe, Mulungu wamupatsa iye njira yogwirira ntchito ndi anthu omwe ine sindikanakhoza kuwakhudza. Ndipo mwinamwake ine ndimagwira ntchito ndi anthu omwe iye sangakhoze

kuwakhudza. Koma, palimodzi, ndife abale tikuyesera kuchita zomwe ife tingakhoze kwa Ufumu wa Mulungu. Mwaona?

⁴² Ndipo masomphenya ndi gawo chabe la Uthenga umene ukulalikidwa. Tsopano, inu mukuona, ngati ine ndikadakhala nawo maphunziro ndi mwinamwake kukhala ndi liwu labwino, ndi zina zotero, ndi kumakhoza kuupereka Uthenga, mofanana, ine mwina ndikanakhala—mlaliki wa mtundu umenewo. Koma, Mulungu podziwa kuti sindikanati ndikhale wophunzira, Iye anachita kundipatsa ine chinachake choti ndizigwira nacho ntchito, inu mukuona. Ndipo ndi momwe Iye anachitira izo, chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa.

⁴³ Tsopano, inu mukhoza kudabwa zomwe zimachitika pa nsanja. Pamene w—w—wodwala kapena... Ine sindikanati ndinene izo mwanjira iyo. Izo zachuluka kwambiri mu kayankhulidwe ka zamankhwala. Nditati ine ndinene, pamene mzanga akuima pamaso pa ine, akufuna thandizo, izi ndi zomwe zimachitika. Ine sindimakhala ndi kanthu kochita nazo izo, osati kanthu kamodzi. Ndi wodwalayo mwiniwake amaigwiritsa ntchito mphatso Yauzimu iyo. Ine sindimakhala ndi kanthu kochita nazo izo, konse. Ine ndimangopitiriza kudzipereka, kudzipereka, mpaka mzimu wawo ndi Mzimu umene uli pa ine, umene ine ndikudzipereka kwa iwo, mpaka Mzimu Woyera...

⁴⁴ Ine ndizitcha izo ichi, kuzipanga izo mwanjira iyi, kani, chotero kuti inu mumvetse. Pano pali Mzimu Woyera pamwamba *apa*, ndiyeno ine ndimangopitiriza kudzipereka mwiwanga kwa Iye, mpaka ine nditadziwa kuti Iye—Iye ali pamenepo. Ndipo ine ndimayankhula kwa munthuyo mpaka ine nditagwira tcheru chawo. Mpaka apo, ine sindimadziwa kena kalikonse. Ndipo Mzimu Woyera, chifukwa cha mzimu wanga pokhala utadzipereka, umandisonyeza ine moyo wawo. Ndipo pamene izo zichitika, izo zimamanga chikhulupiriro cha wodwalayo, mpaka pa malo monga awa.

⁴⁵ Ndipo nthawi zambiri, ndiye, ine ndikayamba kunena chinachakenso, Iwo umandiyimitsa ine ndi kuti, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Tsopano muzizipenya izo. Ndizo zangwiro, nthawi iliyonse. Iwo sunayambe walepherapo. Iwo umawauza iwo basi zomwe zikukonzekera kuti zichitike. Ndipo izo zimakhala mwanjira imeneyo. Muzizilemba izo, ndi kuwona ngati izo siziri mwanjira imeneyo.

Tsopano, izo, wodwalayo akuzichita izo.

⁴⁶ Tsopano ine ndikhoza kungopereka izi mu mawonekedwe aang’ono ophunzira, kotero kuti inu mukhoze kumvetsa. Titi, apo, pali waukulu wamphamvu... Ndife tonse anyamata aang’ono ndi asungwana, ndipo ife tiri pansu ku... mmbuyo mu nthawi ya unyamata. Ndipo pali mpanda waukulu kwambiri apa. Muli chionetsero mkatimo. Ndipo ine—ine ndangopezeka kuti ndine wamtali pang’ono kuposa inu. Mwinamwake inu

ndi amphamvu kuposa ine, koma ndine wamtali. Mukuona? Mulungu amawapanga anthu mwanjira yosiyana kwa ntchito zosiyana. Chabwino, ndiye, pamwamba *apa*, basi cha pamene ine ndingakhoze kuyang'ana kupyolerapo, pali bowo mu khoma. Chabwino, tsopano, ine ndikhoza kufikira pamwamba, chifukwa ine ndimafikira patali pang'ono, ndipo ndikhoza kudzikokera pamwamba, pa zala zanga, ndikuyang'ana kupyolera mu bowo ili. Ine ndibwerera ndi kukuuzani inu zomwe ine ndinaziwona. Inu mukumvetsa lingalirolo tsopano? Inu mukunditsatira ine? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

47 Tsopano, tsopano, mwinamwake munthu wotsatira, iye ndi wamphamvuko, koma iye sangakhoze kuwona utali woterowo. Kotero iye akuti, "M'bale Branham, kodi inu mukuona chiani?"

48 Ine nkuti, "Mphindi yokha." Ndipo ine nkulumphira pamwamba, mokwera kwenikweni, ndi kugwiritsa zala zanga pa mapeto, ndi kudzikokera ndekha pamwamba, molemera kwambiri. Ine nkuti, "Ine ndikuwona njovu." Ndipo ine nkutsika pansi. Mwaona? Ndi zothetsa mphamvu, chifukwa ine ndikudzinyamulira pamwamba. Ine ndikunena izi ngati mwa fanizo kotero kuti mutsimikize kuti mukumvetsa.

Tsopano, pamene ine ndibwerera pansi, "Kodi inu munawona chiani?"

"Njovu." Mwaona? Chabwino.

49 Tsopano, izo ziri ngati munthu ataima pa nsanja, akugwiritsa ntchito mpatso Yauzimu. Ndipo ndi cholemetsa, chifukwa munthu iyemwini akuigwiritsa ntchito mpatso iyo. Iwo samazindikira izo, koma iwo akuigwiritsa ntchito iyo, iwoeni.

50 Tsopano, ine ndinauzidwa usiku watha kuti panali bambo anaima pa nsanja. M'bale Joseph anandiuza ine, iye atakomana nane, kuti bamboyo anali. . . Poyamba, pamene iye anabwera pano, ndipo ine ndimaganza kuti iye anali wogontha ndi wosayankhula. Ine ndinati, "Inu muli bwanji, bwana?" Chinachake mwa dongosolo limenelo. Ine ndikhoza kusanena mobwereza bwino izo. Ine ndikutenga zomwe iwo anandiuza ine. Ine sindinainvetsere tepiyo panobe. Ndipo anati bamboyo anangoima apo. Ine ndinati, "Chabwino, mwinamwake iye ndi wosamva ndi wosayankhula."

51 Ndipo tsopano penyani chisomo chamwachokha. Mukuona? Ndizo monga wamisala pa nsanja. Ndizo zonga ng'anga mu Afrika, ataima apo ali ndi mafupa mu zala zake, kuti akutsutse iwe, inu mukuona. Chisomo chimagwira apono. Inu simumasowa kuti muzidandaula. Musatero. Palibe chodandaulitsa pa izo. Chisomo chimagwira. Mulungu amagwira pamene inu simungagwire. Ndiyeno pamene bamboyo anaima apo. Ndisanati. . . ine—ine ndinati, "Chabwino, mwinamwake iye

ndi wogontha ndi wosayankhula.” Ndipo zonse mwadzidzidzi, apo panawoneka masomphenya patsogolo panga. Ndiye. . .

⁵² [Belu la wotchi likumveka—Mkonzi.] Tsopano, mukhululukire kulira kwa wotchi uko. Iyo inali yoti ndibwerere kuno ndi kudzayambirapo. Chotero, ine ndikudziwa kuti inu mwatolapo china apo. Iwo amandipatsa ine wotchi uko, yomwe imalira. Kotero, iyo si nthawi yolekezera panobe, ine ndikuyembekeza. Kotero mu. . .Ine ndimvapo za izi; musati mudandaule.

⁵³ Kotero, ndiye, bamboyo ataima apo. Masomphenya, ine mwamsanga, mwinamwake, ndinawona Finland kapena chinachake. Ine sindiri kukumbukira. Koma tsopano, chirichonse chomwe chinali, iwo anati ine ndinamuza iye kuti iye anali wachi Finn. Ndipo iye akutipusitsa ife, chinachake chimzake, mwinamwake iye anali wachi Finn. Chabwino, Joseph kuno, anati iye akanakhoza. . .Icho chinali chododometsa kwa iye, momwe Iwo ukanadziwira fuko lomwe bamboyo anali wa ilo. Mulungu mu chisomo Chake anasonyeza izo.

⁵⁴ [M'bale Joseph Mattsson-Boze akuyankhula ndi M'bale Branham zokhudza m'bale wachi Finish yemwe anachiritsidwa.—Mkonzi.]

⁵⁵ Ine ndikudabwa ngati izo ziri mwa mwayi kuti bamboyo angakhale ali mchipindachi lero, ndi ngati winawake wakhala pafupi naye, yemwe angakhale ngati. . .ngati iwo angakhoze kuyankhula chi Finnish, mungati—mungawone ngati kuli kulondola. Kodi inu mungakweze dzanja lanu, ngati bamboyo ali mchipindachi, lero, bambo wachi Finnish yemwe anali muno usiku wathawu, yemwe ife tikumukamba, amene anali pa nsanja. Ine ndimangofuna—ndimafuna. . .

⁵⁶ [M'bale Joseph Mattsson-Boze akupitirira kuyankhula ndi M'bale Branham za m'bale wachi Finnish yemwe anachiritsidwa.—Mkonzi.] Chabwino, uyo, ine ndikulingalira iye anabwerera, mwina, kumudzi kwawo.

⁵⁷ Tsopano, tsopano, pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, ndipo. . .Iye anali kamwa yoyankhulirapo yodzozedwa ya Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anali—Mwana wobalidwa yekha wa Mulungu. Ndipo Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjantsira dziko kwa Iyemwini, mopanda muyezo. Inu mukukhulupirira izo, ophunzira Baibulo? [“Ameni.”] Iye anali Emmanuele. Palibe aliyense wa ife ati adzafikepo konse pa malo amenewo. Ayi. Ayi. Iye anali Mwana woyera wobadwa kwa namwali, ndipo ife sitidzakhala konse. Sitidzakhoza konse kuchita zinthu, zonga izo, chifukwa Iye anali Icho.

⁵⁸ Koma tsopano Iye analonjeza kuti zinthu zomwe Iye ankazichita ife tizidzazichita nafenso, chifukwa ife tikanadzakhala ana okhazikitsidwa kwa Mulungu,

kupyolera mwa Iyeyo. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, izo si...Ndizo za aliyense wa ife. Wokhulupirira aliyense amakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndi kulondola uko? [“Ameni.”]

⁵⁹ Tsopano, pamene mkazi wa vuto lamagazi anagwira chovala Chake, izo zinali basi monga kusuzumila kupyolera pa chibowocho. Mwaona? Iye anamverera mphamvu zitachoka pa Iye. Iye—Iye anafooka, koma Iye sankadziwa chomwe chinachitika. Winawake anali atamugwira Iye, ndi c—chikhulupiriro. Ndipo Iye anafunsa yemwe anali, ndipo aliyense anakana izo. Kotero ndiye nchiani chinachitika Iye atachita izo, bwanji, Iye anayang’ana pozungulira mpaka Iye anamupeza. Tsopano, pali...

⁶⁰ Kodi Iye anamudziwa chotani iye? Ndilo funso lomwe ine ndikufuna kuti ndirifikitse kwa inu. Kodi Iye anamudziwa chotani iye? Tsopano ndiroleni ine ndiyesere, ndi...monga m’bale, kuti ndifotokoze izi, momwe Iye anamudziwira iye.

⁶¹ Chifukwa, pamene aliyense wachita izo, ine ndikhoza kunena kuchokera pa misonkhano kuno, kuchokera pa kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera. Pamene wina aliyense wadalitsidwa kumene, izo zimangowoneka ngati kuti ndi chinachake chikukukoka iwe, monga *choncho*, onani, ndipo iwe umafika kwa munthuyo. Ndiyeno, basi pamwamba pa munthuyo, iwe umaziwona izo ndi zomwe zachitika kwa iwo, ndi zomwe ziri zovuta ndi iwo. Ndiyeno iwe umayang’ana, ndipo iwe umawona kuti ndi munthu yemweyo, ndi basi monga—mpita kapena modzera momwe zikugwirira ntchito pakati pa iwe ndi munthuyo.

⁶² Ndi momwe ine ndikuganizira. Iye sanazifotokoze konse izo. Ndi momwe ine ndikuganizira kuti Iye ankadziwira izo. Chifukwa, Mzimu Woyera umagwira ntchito mwanjira yofanana, ndi momwe izo zimamvetsedwera.

⁶³ Titi, monga nthawizina iwe umati, “Dona wakhala apo, yemwe wavala chisoti chobiriwira,” kapena chinachake monga *choncho*, “inu mwakhala mukuvutika ndi *zakuti-n-zakuti*. Inu mukuchokera ku malo *akuti*.” Inu mukumvetsera kwa izo. Mukuona? Iwe uli mu masomphenya momwe, ukupenya zomwe zikuchitika. Ndiyeno mwinamwake iwe umamuwona iye akubwerera mmbuyo, ndi kuwala kuli pomuzungulira iye, ndi chirichonse. Bwanji, ndiye iwe umati, “Bwanji, iye wachiritsidwa. Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.” Mwaona? Ambuye Yemwe akuwonetsa masomphenya, ndi chikhulupiriro chanu basi mwa Iye, akundigwiritsa ine ntchito ngati kamwa yoyankhulira kuti ndinene kwa inu zomwe inu mukukhumba kuti Iye akuuzeni inu. Mukuona zomwe ine ndikutanthauza? Tsopano, koma pamene izo ziri zinazo...Tsopano, iyo

imangokhala njira yongokuloleza ya Mulungu, ikugwira ntchito.

⁶⁴ Ine ndikunena izi molemekeza. Ora liri pafupi kwambiri, pamene, ine ndakuuzani kale chomwe masomphenya a Ambuye andisonyeza ine, kuti izi potsiriza zidasunthira mmbuyo, kupereka malo kwa chinachake cha patali mopitirira ichi. Ndipo ndicho chimene ine ndikufuna kuti ndifike kwa icho, madzulo ano.

⁶⁵ Tsopano, munthu pochita izo, adza—adza, ngati iwo angazikhulupirire izo, iwo amadalitsidwa ndipo iwo amachira. Tsopano, osati ngati iwo anali kuchiritsidwa; koma chikhulupiriro chawo chinamugwira Mulungu ndipo analandira machiritso awo omwe anaikidwa kale kwa iwo, zaka naintini handiredi zapitazo. Mwaona? Sikuti izo zinali ndi kalikonse kochita ndi machiritso awo. Iyo yangokhala kamwa yoyankhulirapo, kuti iziyankhula.

⁶⁶ Ankachita motani mu malo aliwonse mu Baibulo? Ife sitiri... Ine sindiri kudzifanizitsa ndekha ndi mneneri. Ayi, bwana. Ayi. Ine ndangokhala wochimwa wosauka wopulumutsidwa mwa chisomo. Koma mphatso yomwe Ambuye ankawapatsa aneneri, kuti iwapange kukhala aneneri, iwo anali kamwa zoyankhulirapo Mulungu. Iwo anali nawo Mawu a Ambuye. Ndipo palibe mneneri anayamba wachitapo chirichonse mwa kukhamba kwake kwake. Iye ankachita izo, poyamba, Mulungu atamuza kaye iye. Ndiko kulondola.

⁶⁷ Ndipo ndi momwe Mwana wa Mulungu, pamene Iye anadza, chomwe anali Mulungu wa mneneri. Iye anati, “Ine ndimachita kokha monga Atate andisonyezera ine kuti ndichite.” Ndiko kulondola. Izo zimayenera kokha kuti zizibwera kupyolera mu mphamvu Zauzimu, kuti aulule kupyolera mu mnofu. Ndipo Khristu anali kamwa yoyankhulirapo Mulungu pa dziko lapansi. Aliyense akuzimvetisa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁶⁸ Tsopano, mwa chitsanzo, nthawizina, ine ndikhoza kukhala ndiri kunyumba. Gene, Leo ndi iwo omwe ine ndimawakamba usiku watha, akhala mmusi umu, M'bale Beeler ndi ambiri a ena onse a iwo, ndi iwo omwe amandidziwa ine. Kunyumba, ine ndimakhoza kukhala ndikuyenda kudutsa nyumba, ndisakulingalira za chirichonse. Mwinamwake nditakhala pansu mu chipinda, ndipo apo pamabwera masomphenya. Ndipo mwinamwake iwo nkukhala bata mwangwiro kwa kanthawi pang'ono. Ndipo iwo nkuti. . .

⁶⁹ Iye nkuti, “Tsopano, iwe uyitanidwa mu mphindi zochepa, pa foni, ndipo iwe upita ku mzinda *uwu*. Ndipo pamene iwe uti upite ku mzinda *uwu*, iwe ukapita ku malo *ena ake*. Izo zikakhala mwanjira *iyi*. Ndipo iwe ukalowa mchipinda, ndipo iwe ukaika chipewa chako pansu. Kapena, dona akaika chipewa chako pa kama, koma icho sichikuyenera kuti chikakhale chiri apo. Icho

chikuyenera kuti chikakhale chiri pa gome apo, ndipo dona wina akabwera kuchokera *uku*.”

⁷⁰ Iwe ukaziwona izo zonse zikuseweredwa ndendende basi momwe izo ziyenera kuchitiridwa. Ndipo ngati ine ndilephera mu chimodzi cha zinthu izo, izo sizikachitika. Izo ziyenera kuti zikakhale ndendende basi ku mphindi ndi nthawi, ndi chirichonse mwapamalo ake chimodzimidzi, chifukwa ndi masomphenya. Izo—izo ziyenera kuchitika mwangwiwo. Ndiyeno pamene izo zitero, izo ziyenera kuchitika. Izo sizinayambe zalepherapo. Tsopano, ndi pamene Mulungu akuigwiritsa ntchito mphatso Yake. Izo sizimandifooketsa ine. Izo sizindivutitsa ine.

⁷¹ Tsopano, pamene Yesu anamuukitsa Lazaro kuchokera mmanda, zinali patali kuposa chozizwitsa kuposa zomwe mkazi anachita yemwe anakhudza chovala Chake ndipo anachiritsidwa ku vuto lamagazi. Kodi inu mukuvomereza izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye sananene konse mawu amodzi za kufooka, ndi ukoma kuchoka mwa Iye, chifukwa Mulungu anali akuigwiritsa ntchito mphatso Yake. Mwaona? Ndi masomphenya a mtundu umenewo. Ndi mtundu uwo wa masomphenya.

⁷² Koma pamene anthu ayigwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu, ndi chimene chimandipangitsa ine kufooka ndi zotero, pa nsanja, ndiinu enianu. Ndi chomwe chimachita izo. Inu enianu mumaichita ntchitoyo, kuigwiritsa ntchito, ndicho chifukwa ikumachita kukoka. Ndi mwina inuyo mukuigwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu, kapena Mulungu akuigwiritsa ntchito mphatso Yake.

⁷³ Tsopano, pofanizitsa, ine ndingati... Ngati inu mutandifunsa ine, “Kodi muli chiani umo?”

“Chabwino, ndi nswala.”

⁷⁴ “Ndi chiani chinanso chimene inu munachiwona? Chiani...” Ndikutopa, mukuona, ndi chinachake chimene iwe ukuchiwona.

⁷⁵ Koma tsopano pamene Mulungu akufuna kuti iwe udziwe chomwe chiri kuchitika, Iye amangokunyamulira iwe mmwamba ndi kukukweza iwe pamwamba pa chinthu chonsecho, ndi kuti, “Zochitika zonse ndi izi. Mukuona? Chithunzi chonsecho ndi ichi. Iwe ukachita *izi*, ndi kuchita *izi*, ndi kuchita *izi*, ndi *izo*.” Nkukukhazikanso iwe pansi. Iye anali atakunyamulira iwe mmwamba, ndi mikono Yake ya nthawi zosatha ndi mapiko. Ndipo mulibe kanthu mu dziko... Iwe ukabwerera pansi, iwe umamverera ngati ufuule ndi chigonjetso. Koma ndi zimenezo.

⁷⁶ Tsopano, anthu ambiri, iwo amaganiza kuti winawake yemwe amawona masomphenya ayenera kukhala ali Wauzimu. Ayi, bwana, osati mwa njira iliyonse. Ayi, bwana. Palibe wina

Wauzimu koma Mulungu. Ndizo zonse. Ndipo palibe aliyense. . . Mulibe kusiyana mwa aliyense wa ife. Ndife tonse ochimwa, opulumutsidwa mwa chisomo. Ndipo wina sali pamwamba pa mzake. Kungoti, wina anapatsidwa chinachake, ndipo iye adzayenera kuti adzayankhire pa chimene iye anachita ndi luso lomwe linapatsidwa kwa iye. Ndiko kulondola. Munthu aliyense ayenera kuyankhira kwa izo.

⁷⁷ Tsopano, ine ndikhoza kukuuzani inu masomphenya omwe angochitika kumene. Ndipo kotero kuti. . . M'bale Joseph anandipempha ine kuti ndichite izi, chotero kuti anthu omwe ali muno mu nyumbayi omwe sakanakhoza kumvetsa n—nkhani ya mmagazini iyi, akhoze kumvetsa. Ine ndinapanga. . . Pamene ine ndinakhala koyamba w—wantchito wa Ambuye, kuti ndizipempherera ana Ake odwala, inu mukuidziwa nkhaniyo, momwe Iye anandiuzira ine kuti ine ndinabadwira kuti ndizipempherera anthu odwala.

⁷⁸ Tsopano, inu mukuti, “O, ine ndazimva izo nthawi zochulukana, ndi anthu osiyana.” Izo zonse nzabwino. Mwaona? Kuti, iwo, ine—ine sindingakhoze kuyankhira za winawake. Ine ndiyenera kuyankhira pa zanga zanga, ndipo inu muyenera kudzayankhira pa zanu. Tsopano izo ndi zoonaka.

⁷⁹ Ndiyeno pamene Iye anandiuzira ine izo, ine ndinadziwa kuti zinalipo, mu utumiki uwu, pakanadzayenera kukhala pali zinthu zochulukana zoyenera kuzilingalira; ndalama, mwa chinthu chimodzi. Chabwino, ine ndinapanga lonjezo kwa Mulungu, kuti sindikanamadzatenga ndalama za anthu. Ndipo ine ndinamupempha Iye. . . ine sindinkafuna ndalama za anthu, koma ine ndinkadziwa, mmenemo, pakanati padzakhale ndalama zambiri zizidzaperekedwa kwa ine, ndipo ine ndikanadzayenera kumadzazikana izo. Kotero, ine ndinamuuza Iye, bola ngati Iye angamandilemeretse mu njira zanga, kotero kuti ine ndisamadzati ndizidzapempha ndalama, ine ndikanadzakhala ku ntchitoyi bola ngati Iye azindilemeretsa ine. Koma pamene Iye adzafika poti Iye wandilephera ine, mpaka pamene ife tizidzachita kumapempha, kapena kutenga maora, kapena chirichonse chomwe iwo amachita kuti atenge zopereka, monga ine ndaziwonera izo nthawi zambiri mu chipembedzo changa chomwe cha mpingo umene ine ndinalimo apo, ndiye ine ndinati ine—ine ndikanadzachokako ku ntchitoyi. Iye anandidalitsa ine kwa pafupi zaka naini. Koma mu California izo. . .

⁸⁰ Utumiki wanga, unkawoneka ngati, unkawamba kutsika pansu, mwanjira yina. Makalata anasiya. Zinkawoneka ngati anthu sanali kukondweretsedwa. “Chabwino,” ine ndinaganiza, “Mulungu, izo zonse ziri mdzanja Lanu.” Kumene, ine ndinkakhoza kulandira pafupi makalata sauzande pa tsiku, kapena chinachake monga izo, ndi kukhala pamene, ankakhoza kutsika mpaka pa sikisi handiredi, kenako faifi

handiredi, ndiye kutsika mpaka ku foro handiredi, firii handiredi, handiredi, mpaka sevente-faifi, cha pamenepo. Kutsika mpaka pafupi monga choncho, pa tsiku, makalata sevente-faifi pa tsiku, mwinamwake.

⁸¹ Chabwino, ine ndinaganiza, “Chabwino, ndikudabwa chomwe chachitika? Ine sindikudziwa ngati ine ndachita chirichonse. Ngati ine ndatero k—kwa, kwa anthu, bwanji, i—i—ine ndikupepesa.” Ndithudi, ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndiribe. . . Ine sindimagulitsa zinthu. Ndipo chinthu chokha chomwe anthu amalemba kwa ine ndi kuti apeze tinsalu tapemphero. Ndipo ife sitimagulitsa izo. Ife timapereka izo kwa iwo. Kotero, chabwino, Ambuye, mwinamwake Inu mukukonzekera kuti musinthe zinthu.”

⁸² Ine ndinapita ku California, ndinalowa pafupi—pafupi mu ngongole ya madola fiftini sauzande, mu msonkhano. Ndipo usiku umenewo, pamene ine ndinkachoka, ine ndinamufunsa Billy kuti andiuze ine. Ndipo anthu okonedwa omwe anali kuthandizira izo, iwo anathandizira izo, ndipo zinali zabwino kwambiri, ambiri. Koma ilo silinali lonjezolo. Ine ndinamulonjeza Mulungu zomwe ine ndikanati ndidzachite.

⁸³ Ndipo pamene m’bale wokonedwa ananditengera ine kunyumba usiku umenewo, kuti ndipite ku nyumba ya mitengo yaing’ono kumene ine ndinali kukhala, ine ndinapita pamwamba pa phiri, kwa ndekha, pafupi thuu koloko mmawa. Ndipo ife tinali oti tichokako pafupi hafu pasiti foro. Ndipo ine ndinapemphera, ndi mwezi ukuwalira pansu, mowala. Ine ndimakhoza kuziwona izo. Izo zinali pa kulakatika masamba kwathaku. Ine ndinati, “Atate Akumwamba, tsopano i—ine ndikuchoka ku ntchitoyi. Ine ndikupita kwathu. Ndipo chirichonse chimene Inu mukufuna kuti ine ndizichita kuyambira pano mpakana, Inu muzingondiululira ine.”

⁸⁴ Ndipo kotero ine sindikanakhoza kumuza Billy ndi iwo. Ine sindimafuna kuti ndiwauze iwo, sindinkafuna kuti ndimuze mkazi wanga. Koma ine ndinati, “Ine ndikawauza iwo pamene ine ndikafika ku Arizona.” Chabwino, ndiye ine ndinati, “Ine ndiyembekezera mpaka ine ndikafike ku mzinda wakale wabwino waku Texas, kumene amayi anga anachokera.” Ine ndinati, “Ine ndikawauza iwo uko.” Ndiyeno ine ndinakafika uko. Ine ndinawauza iwo pamene ine ndinkafika mu Jeffersonville, Indiana.

⁸⁵ Chabwino, Billy, iye anati, “Adadi, muyenera kusamala pa zomwe mukuchita.” Anati, “Kodi Baibulo silimati, ‘Tsoka kwa ine ngati ine sindilalikira Uthenga?’”

⁸⁶ Ine ndinati, “Ine ndikumvetsetsa za kulalikira Uthenga. Ine ndikutanthauza utumiki wauvangeri.” Ndipo ine ndinati, “Taona, Billy,” ine ndinati, “Mulungu ali nawo amuna pa ntchito, kulikonse. Iye sakundisowa ine kumeneko. Ine ndikhoza

kubwerera ndi kukapeza ntchito yanga kachiwiri, n—ndi kupita kumakachita ubusa, ndi kumachita ubusa pa kachisi, kapena chinachake. Ine ndikhoza kupita uko, kumakachita rendi mochitira masewero mwakale kumusi uko, nkumakakhala ndi kusonkhana kwa Lamlungu madzulo kwa aliyense kwa a maiko onse, ndi kuwulutsa kwa pa wailesi kapena chinachake.” Ine ndinati, “Ine sindingakhoze kuimitsa, zonse mwakamodzi tsopano, chifukwa zolipira zanga zimakwana pafupi madola handiredi pa tsiku, ku nyumba. Kotero, ine—ine sindingathe, ndi ofesi yanga ndi zinthu.” Ine ndinati, “Ine sindingakhoze kungotseka kumene, chifukwa ine sindingakhoze kuchita izo.”

⁸⁷ Ndipo kotero mkazi wanga anati, “Billy, ine ndikuyembekeza iwe ukudziwa zomwe iwe ukuzikamba.”

Ine ndinati, “Chabwino, tsopano, i—ine ndikudziwa chinthu chimodzi.”

⁸⁸ Pamene ine ndinabwera kuno nthawi ina mu msonkhano waukulu, kudzakhala ndi msonkhano waukulu, ndipo inu mukuidziwa nkhaniyo, chifukwa ine ndinamulonjeza mzanga wokondedwa wamng’ono wachi Swede uyu kuno, M’bale Boze, kuti ine ndikanabwera ndi kudzamulalikirira masiku awiri iye, mu Mpingo wa Philadelphian, utatha msonkhano waukulu uwo. Ine ndinauzidwa, ngati ine sindikanatero; ngati ine ndikanachita izo, ine sindikanakhala wodzayankhula. Ine ndikhoza kutenga kusankha kwanga. Ine ndinati, “Ine ndikhala ndi mawu anga.” Ndipo ine ndinapita kwa M’bale Joseph. Ndendende. Chifukwa, ine ndikanati ndidzachite izo kachiwiri. Munthu yemwe sangasunge mawu ake si wabwino kwambiri.

⁸⁹ Umo ndi momwe ine ndimamutengera Mulungu. Iye amapereka Mawu, ndipo ine ndimakhulupirira Mawu aliwonse a Iwo. Ndipo ngati Iye akanati asamasunge Iwo, Iye sakanakhala ali Mulungu, kwa ine. Ine. . . Iye ayenera kuti azisunga Mawu Ake, ine ndikukhulupirira. Ndipo Iye azichita izo, ndipo ine ndikudziwa Iye azitero. Tsopano, ndiye ine. . .

⁹⁰ Usiku uwo, ine ndinapita kukagona pamene ife tinafika kunyumba. Mkazi wanga anali akulira. Iye anati, “Billy, ine ndikuchita mantha iwe ukulakwitsa.” Anati, “Iwe ukudziwa ine ndimafuna kuti iwe uzikhala pakhomo ndi ana ndi ine. Koma,” anati, “Bill, taona chomwe izo zapanga. Izo zayambitsa chitsitsimutso cha mdziko lililonse, ndipo ine sindikukhoza kuwona pamene Mulungu angakubweretsere iwe umo, nkukuchotsa ku ntchitoyo.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndinamulonjeza Iye. Iye anati. . .”

“Koma—koma—koma Iye sanakuuze konse iwe.”

⁹¹ Ine ndinati, “Koma, ine ndinamulonjeza Iye. Mwaona? Ndi zimenezo. Ine ndinamulonjeza Iye. Ine ndisunga mawu anga kwa Iye. Ngati ine ndingawasunge iwo kwa m’bale wanga,

ine ndithudi ndingawasunge iwo kwa Mpulumutsi wanga.” Kotero ine ndinalowa umo ndipo ndinagona bwino kwambiri mu usikuwo.

⁹² Mmawa wotsatira, pafupi sikisi koloko, ife tinawuka. Ndi—ndipo ndinali ndikungochokera kogona. Iye anali ali ku mbali ina. Ine ndinali ndikungopukuta nkhope yanga, monga *chonchi*. Ine ndinati, “Chabwino, ine ndiwaimbira a Public Service Company lero, ndi kuwafunsa ngati ine ndingakhoze kupezanso ntchito yanga yakale kachiwiri.” Ndipo ine ndinati, “Ngati iwo sandipatsa ine ntchito yanga, Bambo Woods ndi wazomanga, ine ndizingopita ndi iye. Ndipo iye ndi ine tizipita ndi kumagwetsa nyumba zina, kapena chinachake. Ndipo ine ndiyenera kumagwira ntchito, chifukwa ine ndiyenera kumapita ku ntchito. Ndipo kotero, chifukwa ndalama izi ziyenera kuti zipezedwe, ndipo ine ndiri mu ngongole ya madola fifitini sauzande.” Ine ndinati, “Ndiye nanga ndingachite chiani? Ine ndiyenera kuti ndiziripirensa izo, ziribe kanthu momwe iwo anathandizira pa izo, ine—ine ndibweza polipira izo. Ndiko kulondola.”

⁹³ Ndipo kotero iye anati, “Iwe uwaimbira Bambo—Bambo Bar, mmawa uno?”

⁹⁴ Ine ndinati, “Eya. Ine ndiwaimbira iwo ndi kuwafunsa iwo ngati ine ndingakhale nayonso ntchito yanga. Ndipo ngati iye . . . Ngati ntchito imeneyo, winawake waitenga iyo tsopano, ndipo iwo sangakhoze kumupatsa iye ntchito yabwinoko,” ine ndinati, “ndiye ine basi . . . ndizipita ndi M’bale Woods, ndipo ife tizipita kumakamanga manyumba kapena chinachake chimzake. Ine ndizimuthandizira iye.” Ndipo chotero ine ndinati, “Ngati ine ndichoka ku ntchitoyi, ndithudi, izo zimuchotsa iye, aponso, ndipo iye akhoza kubwereranso ku zomanga, ndipo ife tikhoza kumapita ku ntchitoyo.” Kotero ndiye monga . . .

⁹⁵ Iye anati, “Chabwino, ine—ine zedi ndikuyembekeza iwe ukudziwa zomwe iwe ukuzikamba, Bill.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine . . .”

⁹⁶ Ndipo ine ndinayang’ana. Akubwera, akusunthira pansu kuchokera ku denga . . . O, ine basi mwinamwake . . .

⁹⁷ Ine sindikuyembekeza kuti inu muzimvetse izi. Koma icho ndi chinachake chimene, pamene ife tidzakomana maso ndi maso ndi Yesu, inu mudza . . . ? . . . pa Mawu.

⁹⁸ Apa panadza chinachake, chikusuntha. Ine ndinawona ana awiri aang’ono, a nkhope zakuda akubwera, akupita mmusi, akukoka ngolo yaing’ono.

⁹⁹ Ine ndinati, “Wokonedwa, tayang’ana, akubwera *apawa*.” Ine ndinali nditapita kale umo apo.

¹⁰⁰ Ndipo iye anati, “Kodi iwe ukuyankhula za chiani?” Ine ndimakhoza kumumva iye, koma ine sindimakhoza kumuyankha iye.

¹⁰¹ Ndipo ana aang’ono awa anali akuyenda akubwera cha kwa ine, aang’ono, okhala ngati a tsitsi lalitali; ndi lakuda, maso okuda; nkhope yabulauni, akubwera, akuyenda kudza kwa ine. Ndipo ine—ine ndinawawona iwo.

¹⁰² Ine ndinayamba kusuntha, nkuwapitirira anawo. Ine ndinawawona Bambo Arganbright, m’bale wanga, yemwe wapitapo kutsidya kwa nyanja ndi ine nthawi zambiri, ndinamuwona iye ataima apo, akuyang’ana pa ine. Ine ndinasuntha mpaka, kwa iye.

¹⁰³ Tsopano, ine ndimakhozabe kumumva mkazi wanga akuyenda akuzungulira mu chipindacho.

¹⁰⁴ Ine ndinena izi mwanjira iyi kuti inu muzimvetse izo. Mwina sati akhale ali mawu oyenera, koma kungoti inu mumvetse. Dera limodzi ilo limene ine ndinalimo, ine ndinasunthira apo kupita mu lina. Ine sindimakhoza kumumva iye akuyenda aponso. Izo zinali atapita.

¹⁰⁵ Ndipo ine ndinamuwona Bambo Arganbright. Iye anali mwanjira yake yachilendo pang’ono, momwe iye amaunyamulira mutu wake ndi kukhala ngati akumwetulira pamene iye amayang’ana pa ine. Ndipo iye anati, “M’bale Branham,” iye anati, “ife taika makadi, ponseponse. Ndipo ife takukonzerani inu njira, kaloweni ndi kukatuluka. Ndipo chirichonse chakonzeka.”

¹⁰⁶ Ine ndinati, “Chabwino, M’bale Arganbright, ine ndidzere njira iti?”

Iye anati, “Zingopitirirani.”

Ine ndinayenda chamtsogolo. Ine ndinawadutsa azitumiki ena.

¹⁰⁷ Ndiye, ine ndinayenda motalikira pang’ono. Ine ndinabwera mu mawonekedwe a chochitika chachikulu, ndi mitundu yonse ya, zinkawoneka ngati, mokhalamo anthu zikwi.

¹⁰⁸ Ndipo basi apono ine ndinamumva winawake akuti, “Msonkhano wathetsedwa.”

¹⁰⁹ “Chabwino,” ine ndinati, “ndani wauthetsa iwo? Zafika motani kuti iwo uthetsedwe?” Ndipo ine ndinali ndikukambirana nawo. Ine ndinati, “Nchifukwa chiani iwo wathetsedwa? Nchiani chachitika?” Ndipo inali mvula ikuwaza.

Ndipo Chinachake chinati kwa ine, “Ndi izi iwe udzadziwa.”

Ndiyeno ine ndinati, “Chabwino, ine sindiri. . .”

¹¹⁰ Ndiyeno ine ndinalowa umo, mopitirira kulowa mmasomphenya. Ndipo pamene izo zinatero, ine ndinali nditaima, inu mukudziwa, nsapato ya mwana wamng’ono, wa

pafupi usinkhu wa chaka. Inu mukudziwa, mabowo aang'ono kwambiri; osati kabuti, koma n—nsapato. Ndipo ine ndinali ndi—ndi chingwe mdzanja langa, ndikuyesera kuti ndilowetse bowo laling'ono la gawo la inchi mu bowo ili, ndi chingwe cha pafupi theka la inchi. Ndikungogwira ntchito molimbikira, kuyesera kuti ndikankhire chingwe icho chilowe, chingwe cha theka la inchi, chidutse pa bowo la eyitifi ya inchi. Ine ndinali ndikungodulira ulusiponsepo, chingwecho, ndikuyesera kuti ndichikankhiremo icho chidutse monga choncho. Ndipo icho chinkakanika basi kuti chichite izo. Ndipo chingwecho chinali chonse chitaphwasuka, pa mapetowo.

¹¹¹ Kotero, apo pomwe ine ndinamumva Winawake akuti, kumbuyo kwanga, “Kodi iwe sukumvetsa kuti iwe sungakhoze kuwaphunzitsa makanda zinthu zauzimu?” Ine ndinayang'ana pozungulira. Ndipo Ilo linali kumbuyo kwanga. Ndipo ine ndinalizindikira Liwu limenelo. Iye anati, “Iwe ukugwiritsa ntchito mapeto olakwika a chingwecho.”

¹¹² Ndipo ine ndinayang'ana pansi pa mapeto a chingwecho ali pansi, mulu waukulu wa chingwe, ndipo icho chinali chitalezedwa kukhala kagawo kabwino ka magawo eyitifi ya inchi mwabwino, kotero icho chikanakhoza kudutsa mu bowolo. Ine ndinati, “Ine ndikumvetsano.”

¹¹³ Ndipo pamene ine ndinafikira kuti ndichitole chingwecho, ine ndinatengedwa kachiwiri. Tsopano, inu muzilembe izi apo. Mudzaziwone izo zikamadzachitika. Mwaona? Ndipo pamene ine—ine ndinayamba kuti ndifikire pansi, ine ndinali nditapita aponso. Ndiye, pamene ine ndinasisimukako, ine ndinali nditaima pa mbali pa nyanja yokongola, chinachake chonga nyanja yanu kunoko mu nthawi ya chirimwe pamene iko kumakhala kokongola kwenikweni ndi kobiriwira. Ndipo apo panali asodziponse kuzungulira nyanjayo, ndipo iwo anali akuwedza, koma iwo anali akugwira tinsomba tating'ono. Ndipo ine ndinayang'ana uko mu nyanja, ndipo mphuta izo zazikulu, zokongola kumeneko, ndipo ine ndinati, “Ine ndikudziwa awa ndi masomphenya, koma ine sindikukhoza kumvetsa za mphuta izo. Koma,” ine ndinati, “inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira, pansi pa mu mtima wanga momwe, ine ndikhoza kuzigwira izo.” Kotero, ine ndinachinyamula chingwecho, koma, mmalo moti icho chikhale chingwe, iwo unali mtengo wowedzera.

¹¹⁴ Ndipo basi pomwepo, Yemwe anali kumbuyo kwanga anati, “Tsopano Ine ndikuphunzitsa iwe kuwedza kwake, momwe ungazigwirire izo.” Ndipo chotero Iye anatenga... Ndipo Iye anati, “Manga apo nyambo.” Ndipo ine ndinaika nyambo apo. Iye anati, “Tsopano uponyere kutali uko,” tsopano mveterani mwatcheru, “kutali uko kwakuya.” Ndipo Iye anati, “Pamene iwe utero, tsopano uyilole nyamboyo imire pansi, poyamba. Ndiye,” anati, “uziyikoka iyo mwapang'ono.” Tsopano, ndiwo ukatswiri wa asodzi weniweni. Kotero ine... .

¹¹⁵ Iye anati, “Ndiye, pamene iwe utero, tsopano, iwe uzimverera kuluma kwina pa iyo, koma usati umuuze aliyense zomwe iwe ukuchita. Uzisunge izo kwa iwemwini.” Ndipo anati, “Ndiye pamene iwe—pamene iwe uzimverera iyo ikuluma kachiwiri,” anati, “uyikoke iyo pang’ono pokha mochepa kwambiri, koma osati molimbika kwambiri,” Iye anati, “ndiyeno izo ziichotsa iyo kwa nsomba zazing’onozo. Ndipo pamene izo zibalalika, izo zizikopa chidwi cha nsomba zazikulu, ndipo izo zidzailuma iyo.” Ndipo anati, “Umo ndi momwe uti udzaigwirire iyo.” Anati, “ndiye, pamene ziti zilume, pa nthawi yachitatu, uyikonze mbeza yako kuti—igwire.”

Ine ndinati, “Ine ndamvetsa.”

Anati, “Koma ukhale bata. Usati umuuze aliyense. Ukhale bata.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino.”

¹¹⁶ Ine ndinali ndi nyambo mu dzanja langa. Ndipo asodzi onse awa anapezeka kuti anali azitumiki, ndipo iwo onse anabwera pozungulira, akumati, “M’bale Branham, ine ndikudziwa inu mukhoza kuzigwira nsomba.”

¹¹⁷ O, ndithudi, izo zinandipangitsa ine kumverera bwino kwenikweni. Ine ndinati, “O, inde, ndine nsodzi. Ine ndikhoza kugwira nsomba.” Ndipo iye anati...ine ndinati, “Tsopano, umu ndi momwe inu muzichitira izo.” Ndipo ine ndinati, “Inu muziiponyera iyo kutali.” Ndipo ine ndinapita kutali komwe, mu—mu madzi akuya. Ine ndinati, “Tsopano, nsomba zazing’ono izo ndi zabwino, abale, koma ife tikufuna zazikulu, naponso.” Ndipo ine—ine ndinati, “Muziwona pamene iyo ikumira pansi. Tsopano onani, ndi izo apo, pafupi basi kumene iyo iyenera kumakhala ili. Tsopano, onani apo, onani apo. Apo, izo ndi nsomba zazing’ono.” Ine ndinati, “Tsopano, pamene icho chiwongola kachiwiri. . .”

¹¹⁸ Ine ndinachipatsa icho kugwedeza kwakukulu kwambiri, ndipo, pamene ine ndinatero, ine ndinakoka nyambo yonseyo kuitulutsa mmadzi. Ndipo pamene ine ndinatero, ine ndinagwira nsomba, koma ine ndinadabwa momwe iyo inapezekera ndi nyambo nkamwa mwake. Chifukwa, zimawoneka ngati khungu linangosupukira pa nyamboyo, pafupi usinkhu womwewo wa nyambo. Ndipo ine ndinaganiza, “O, mai!”

¹¹⁹ Ndipo apo pomwe, Mmodzi uyu Yemwe anakhala akuyankhula, kumbuyo kwanga, anadzaima kutsogolo kwanga. Uyo anali Iye, Mngelo wa Ambuye. Iye anali atawapinda manja Ake. Iye amayang’ana pa ine, anati, “Basi zomwe Ine ndinakuuza iwe kuti usamachite!”

Ndipo ine ndinati, “Inde. Uko nkulondola.”

¹²⁰ Iye anati, “Iwe ukuwona, chikoka choyamba chija chinali pamene iwe unakonda kuika manja ako pa anthu ndi

kumawauza iwo lomwe linali vuto lawo.” Anati, “Chikoka chachiwiri chinali pamene iwe ukanamadziwa zinsinsi za mu mtima, monga ine ndinakuuzira iwe.” Ndipo anati, “Mmalo mozisunga izo kwa iwewekha, iwe umayesera kuti uzifotokoza zonse izo, ndi kumawauza anthu. Ndipo pamene iwe unatero,” anati, “iwe sumadziwa kanthu ka izo, iwemwini. Ndipo iwe ukanakhoza kuzifotokoza izo motani? Ndipo iwe wapangitsa gulu lalikulu la kutsanzira kwachithupithupi kuti kuwukepo, ndipo iwe ukuwona zomwe iwe wazichita.”

¹²¹ Ndipo ine ndinati, “Ambuye, ine ndikupepesa.” Ndipo i—ine ndinati, “O, ine ndikupepesa kwambiri! Ine sindikudziwa choti ndichite.”

¹²² Ndipo ine ndinali ndikukoka chingwecho, monga *chonchi*, ndipo ine ndinali kuyesera kuti ndichiwongole chingwe changa. Ndipo Iye anayang’ana pa ine, anati, “Tsopano, usati udzachipilingizitse chingwe chako, mu nthawi ya mtundu uwu.”

¹²³ Ine ndinaganiza, “Mwinamwake Iye andipatsa ine kuyesa kwina.” Ndipo ine ndinali . . . ine ndinati, “Ine ndithudi ndikhala wosamalitsa.” Ndipo ine ndinali ndikuzengeza chingwe changacho, ndinachiwona icho chikutengekera mmwamba bwinobwino.

¹²⁴ Ndiyeno pamene Iye ananena izo, apo pomwe ine ndinadzimverera ndekha ndikupita mokwera, pamwamba kwambiri. Ndipo pamene ine ndinakakhala pansi, ndiye ine ndinali mkati mwake, ndipo nditaima pamwamba pake, pa hema wamkulu. Ine sindinayambe ndawonapo hema woteroyo!

¹²⁵ Ndipo ine ndinali nditangopanga kuitanira kuguwa, zinkawoneka ngati, pansi pa guwa pomwe. Ndipo pamene ine ndinali pansi apo, ine ndinayang’ana, ndipo apo panali mazana a anthu ataima mozungulira guwalo, akulira, chifukwa iwo anali atamulandira Ambuye Yesu. Ndipo iwo anali akungolira, mokuwa. Ndipo ine ndinati, “O, ndizo zofanana kwambiri nazo, monga choncho.”

¹²⁶ Ndipo mtundu weniweni wa njonda anayenda mpaka ku nsanja, anati, “Pamene M’bale Branham akupuma, mphindi pang’ono zokha,” iye anati, “ife tiyitana mzere wapemphero.” Ndipo anati, “Aliyense yemwe ali ndi makadi a pemphero oyambira ndi nambala *inayake*, aime uko, cha kumanja.” Chabwino, ine ndinazindikira mzere wapemphero, zinkawoneka ngati iwo unapita konse kuzungulira hemayo, ndi kutuluka, ndi kutsika ndi msewu. Mzere wapemphero wotero!

¹²⁷ Ndipo ine ndinayang’ana pamwambapo, pamene apo kunali kumanzere kwanga; ndipo izo zikanakhala kumanja kwanga, ngati ine ndikanakhala nditaima pa nsanjapo, ikanakhala ili mbali *imeneyo*. Panali chidutswa cha chinsaru chitayalidwa pamenepo. Ndipo kuseri kwa chinsaru ichi kunali nyumba, yaing’ono ya mphwamphwa, pafupi mapazi thwelofu

chopingasa ndi mapazi twente mu litali, chinachake monga choncho. Chabwino, ine ndinaimirira ndikuyang'ana pa iyo.

¹²⁸ Ndipo ine ndinawawona iwo akumubweretsa dona pamenepo, pa machira. Ndipo panali dona apo akulemba dzina lake ndi zinthu, ali n...pa—pa pepala. Ndipo kotero panali winawake anabwera ndipo anadzamutenga iye, ndipo anamukankha iye chomodusitsa. Ndipo munthu wotsatira anadza nadzadutsa, anali ndi zindodo. Ine ndimawawona iwo akupita kudutsa mu nyumba yaing'ono iyo.

¹²⁹ Ndipo panja pakepo, donayo anatulukira, akufuula pamwamba pa mawu ake, akukankha machira awa. Ndi... .

¹³⁰ Ndiye apo panali dona wina ku mbali inayo, ankawoneka wokhala ngati mkazi wa tsitsi-lakuda, ndipo iye anati, “Chachitika nchiani?”

¹³¹ Iye anati, “Ine sindikudziwa basi.” Iye anati, “Ine sindingakhoze kukuuzani inu zomwe zachitika.” Iye anati, “Ine ndakhala ndiri wopuwala kwa zaka makumi awiri. Ndipo, taonani, i—ine ndikumverera ngati i—i—ine sindinayambe ndadwalapo.”

¹³² Ndipo nthawi yomweyo, kunjako anatulukira bambo, akutsimphina ndi kumalumphu, ali ndi zake—ali ndi zindodo zake mu dzanja lake. Ndipo ine—ine ndinayang'ana pa izo. Ndipo basi pomwepo... .

¹³³ Tsopano, pano pali chinachake. Zindikirani mwatcheru. Pali kusiyana pakati pa Mngelo wa Ambuye ndi Kuwala kuja. Chifukwa, ine ndinamva chinachake chikusuntha, monga Icho chimachitira pamene Icho chimakhala chikubwera pa nsanja pano, usiku, mokhala ngati “hfuwi, hfuwi, hfuwi,” ndi monga Moto ukumenyetsa mozungulira, malawi onyambita. Ndipo Iwo unandisiya ine, ndipo Iwo unapita mmusi momwe pamwamba pa omvetsera awo, ndipo unapita ndipo unakaima pamwamba pa nyumba yaing'ono iyo, ndiye unakakhazikika pansu pamwamba pakepo. Ndiyeno, pamene Iwo unatero, Uyu yemwe anali ataima pafupi ndi ine, kumbuyo kwanga, Liwu lomwelo, Liwu la Mngelo, Iye anati, “Ine ndidzakakomana nawe mkati umo. Ndipo ichi ndicho chikoka chachitatu, koma palibe munthu ati adzadziwe kanthu za icho.”

¹³⁴ Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine sindikumvetsa. Chifukwa chiani mkati umo? Chifukwa chiani mmenemo?”

Iye anati, “Icho sichidzakhala chowonetsera pagulu, nthawi iyi.”

¹³⁵ Ndipo ine ndinati, “Ine sindikumvetsa, zopita mkachipinda umo monga choncho.”

¹³⁶ Ndipo Iye anati, “Kodi Izo sizinalembedwe ndi Ambuye wanga, Pamene inu mupemphera, musati muzikhala monga achinyengo omwe amakonda kuti azimvedwa pamaso pa anthu.

Koma muzilowa mkachipinda kobisika ndi kumakapemphera kwa Atate Yemwe amawona za mseri; ndipo Iye Yemwe amawona za mseriyo adzakulipirani inu poyera?” Ndi zangwiro kwa Lemba. Nthawi iliyonse, izo ziri.

Ndipo ine ndinati, “Ine ndikumvetsano.”

¹³⁷ Ndiye Iye ananditengera ine ku malo awa, ndipo anadzandikhazika ine pansu mu chipinda ichi momwe ine ndinalimo. Ndiyeno Iye anandiuza ine zoti ndichite kwa nthawi yachitatu. Tsopano, amzanga Achikhristu, izo zidzakhala, pamene ine ndidzachoka pa dziko lino, izo zidzakhala ziripobe mu chifuwa changa. Pamene ine. . . Koma, inu musunge mawu anga, zomwe ziti zidzachitike.

¹³⁸ Pamene, iyo—iyo inali miyezi faifi yapitayo, miyezi sikisi tsopano, ndipo ife tinalibe lingaliro kuti tikanadzapita konse ku—kumusi uko ku Mexico.

¹³⁹ Koma ine ndimaganza kuti ine ndimapita ku Phoenix. Ndipo mzathu wokonedwa ndi m’bale yemwe anali kupempherera odwala, Bambo Allen, iye anapita mmenemo. Iye anati, “Ayi. Ine ndikhala ndiri kuno, kotero ine sindidzachoka mu gawo ilo la mwezi.” Chabwino, ine sindikadapita uko apo, m’bale wanga ali uko. Ine sindikadachita basi izo. Kotero, ine sindikumudziwa M’bale Allan, komabe iye akuchita kumeneko ntchito ya Ambuye. Kotero ine. . . Iwo anati, “Ayi. Iye akhala alipobe.” Ine ndinati. . .

¹⁴⁰ Chabwino, abale anandiyitana ine, b—bungwelo uko, gulu la azitumiki. Pomwe, ine ndimayenera kuti ndikatenge malo a M’bale Roberts pamene iye anali atapita ku Australia. Ine ndinati, “Chabwino, zonse ziri bwino. Ngati iwo ali naye wina kumeneko, M’bale Allen akupempherera odwala, ine sindingati ndipiteko. Izo sizikanakhala zapaubale.” Kotero ine ndinati, “Chabwino.”

¹⁴¹ Ndipo M’bale Arganbright anandiyitana ine, masiku angapo kenako, ndipo anati, “M’bale Branham, ine ndayankhula ndi M’bale Moore. Bwanji osangopita uko mu Mexico?”

¹⁴² Ine ndinati, “O, Baron Von Blomberg ndi ochuluka a iwo ayesera kuti anditengere ine ku Mexico. Ine sindikusamala za kupita uko.”

¹⁴³ Ine ndinati, “Tiyeni tingokhala ndi msonkhano wamu Amereka kwina kwake.” Ine ndinati, “Ine ndimafuna kuti ndidzayike hema uyo uko, kwa nthawi yoyamba.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, bwanji osangopita ku Mexico?”

Ine ndinati, “Chabwino, ziri bwino. Ine ndi. . . Inu muone pa izo.”

¹⁴⁴ Kotero uko kunali munthu wina kumusi uko. Ndipo iye anandiyitana ine ndibwerere, anati, “Msonkhano wonse wakonzedwera kwa masiku omwe omwewo.” Ndipo anati, “Ife

tidzakhala nawo iwo mkati mwa nyumba yoyankhuliramo yaikulu kwambiri kumusi uko.”

¹⁴⁵ Ndipo usiku uwo, ine ndinali kwa Bambo Woods uko. Ine ndinaganiza, “Inu mukudziwa, uko nkulondola. ‘Ana aang’ono, a nkhope-zakuda, owoneka monga Achimwenye,’ ndicho chimene masomphenyawo ali.” Ndiyeno ine ndinati, “Koma, chinthu chodabwitsa, izo zimayenera kuti zikhale mwamukulu, ndi chinachake cha ‘kubalalitsa.’” Kotero ndiye pamene ife. . .

¹⁴⁶ Masiku awiri kenako, Bambo Arganbright anatiitana ndipo anati, “M’bale Branham, ife tapeza bwalo la ng’ombe lalikulu. Ndipo boma la Chimexico likukubweretsani inu umo, kwa nthawi yoyamba w mbiriyakale ya Mexico yomwe wosakhala Mkatolika anayamba wabweretsedwamo ndi boma.”

¹⁴⁷ Kotero ine ndinati, “Izo ndi zodabwitsa.” Kotero ine ndinati, “Tsopano chinachake chikukonzekera kuti chichitike.” Ine ndinati, “Ife tiri ndi vuto lomwe likudza.”

¹⁴⁸ Ndipo inu mukudziwa, pamene ife tinapita uko mu Mexico ndipo titakonzeka, ndipo tinapita ku bwalolang’ombe ilo, winawake. . . Iyo inkavumba, pa ulendo tikupita uko, ndipo winawake anali atabalalitsa misonkhano iyo. Ndipo iwo sakudziwa yemwe anachita izo, panobe. Ndiko kulondola. Ndizo ndendende molondola.

¹⁴⁹ Ndiye ine ndinabwerera kunyumba, ndinauluka kubwerera tsiku lachiwiri lake. Ife sitikanakhoza ngakhale. . . M’bale Moore anati, “M’bale Branham, ine—ine ndifufuza izo.” Ndipo ife sitimakhoza ngakhale kumupeza mtumiki, kulikonse. Ndipo palibe munthu anadziwa kanthu za izo. Ndipo M’bale Moore anati, “Ngati ine. . . M’bale Branham, mochuluka momwe ine ndakutsatirani inu, ngati ine ndikanati ndisamakukhulupirireni inu konse mpaka nthawi ino, ine zedi ndikanatero tsopano.”

Ndipo ine ndinati, “Ndiko kulondola.” Kotero, ife tinabwererako.

¹⁵⁰ Ndiyeno ine ndinamumva kuti Bambo Arganbright ali pa ulendo kubwera kudzandiwona ine.

¹⁵¹ Ine ndinachokapo kuti ndikapemphere ku mphanga yanga, ndi kukawafunsa Ambuye chiani. Iwo anandisonyeza ine masomphenya ena. Iye anati, “Nsomba zakufa.” Zinali ziri apo, ndipo Iye anandiuza ine chomwe izo zinali. Anati, “Bwerera. Koma iyi si kwenikweni nthawi yake, koma ine ndizidalitsa izo.”

¹⁵² Ine ndinabwerera kumusi uko, ndi penapake pafupi anthu forte, fifite sauzande anabwera kwa Khristu. Mwana wakufa anaukitsidwa kwa akufa, ndipo zinthu zazikulu zinachitika.

¹⁵³ Tsopano ine ndikuliyembekezera oralo. Inu mukhoza kulingalira momwe izo zikuwonekera zazing’ono tsopano, kuti zinthu izi zikuchitika, zinthu zazikulu izi zomwe zachitika kale.

154 Usiku wina, ine, ndisakudziwa...Ndi angati anali ku Mpingo wa Philadephan pamene iwo anandimva ine ndikuyankhula kwa munthu winawake, “Akhale wotembereredwa munthu yemwe atautse maso ake pamene ine ndikumupempherera mkazi wakhungu uyu”? Ndi zomwe ine ndinali ndikuchita. Mwaona?

155 Ambuye akukonzekera kuti achezere anthu Ake, mwa chinachake chachikulu, chodabwitsa, abwenzi. Ndipo ine ndingati...Icho chiyenera chikhale chiri chinsinsi mu mtima wanga momwe. Koma monga inu mukundidziwa ine, ndipo inu mukundikhulupirira ine, ndipo mumandikonda ine, ndipo mumandilemekeza ine ngati wantchito wa Mulungu; ingokumbukirani, ine ndikukuuzani inu, mdalitso uli mu njira, ndiko kulondola, ukudza. Ndipo izo sizimandifooketsa. Izo sizidzandifooketsa ine kenanso. Ndipo izo zidzakhala patali kupyola chirichonse chimene chinayamba chachitikapo kuno kapena nthawi ina iliyonse. Ndi chinachake basi chimene Ambuye apereka. Ndipo ine ndikufuna... .

156 Izo zingandipange ine—wokhulupirira mu chisomo. Ine nditatha kuchita, ndipo zinthu zomwe ndinazichita, ndi momwe ine ndinachitira, ndi kutsutidwa pamaso pa Mulungu, ndipo komabe, pamene Mulungu ayankhula chirichonse ndi kupanga... .Iye azichita izo, mulimonse. Amenii.

157 Mose anapha munthu, nthawi ina. Koma Mulungu anali wotsimikiza. Iye anamusunga iye kuseri uko kuseri kwa chipululu, kwa zaka makumi anai, koma iye anatengera Israeli ku dziko lolonjzedwa.

158 Kodi Iye si wodabwitsa? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Iye ali Mulungu yemweyo lero yemwe Iye anali apo. Ndipo, abwenzi, ine ndikunena izi kwa inu, aliyense wa Akhristu okhulupirira inu, mosasamala mpingo umene inu mumapitako.

159 Uko mojambulira, tsiku lina, kunali munthu. Ine ndinali kuyankhula kwa iye, munthu wabwino kwambiri ndi mkazake, kumene M’bale Boze ndi ine tinali kupanga zojambula zina zoti ziwulutsidwe. Ndipo iye anali akugwedeza dzanja langa ndi kumayankhula. Ndipo ine ndinati... .Chabwino, iye—iye amamukonda M’bale Joseph mochuluka kwambiri. Ine ndinati, “Kodi inu... .Inu mumapita ku mpingo wake?”

Iye anati, “Ayi. Ndine wa Methodistii.”

160 Ine ndinati, “Chabwino, inu mukhoza kukhululukidwa chifukwa cha izo.” Ndipo kotero ine ndinkangomuseleula iye, monga choncho. Ndipo ine ndinati, “Ine ndinali kungopitiriza, kwa inu.”

161 Ine ndinati, “Taonani, m’bale, ine ndinkakonda kuchita za kukwera pang’ono. Ndipo abambo anga anali wokwera.” Ndipo ine ndinati, “Kumtunda uko ku Nkhalango ya Arapahoe,

kumene ife tinkadyetsa ng’ombe,” ine ndinati, “iwo... Kulibe chinthu china chomwe chikanabwera ku chigwa icho kupatula mtundu weniweni wa Hereford, mwamtheradi. Woyang’anira ankaima pa mpanda wa kuchigwacho ndipo sankakhoza kulola iliyonse kupatula iyo itakhala yolembetsedwa, mtundu weniweni wa Hereford.” Ndipo ine ndinati, “Zina zomwe zinkabwera uko zinali Lazy J., zina zinkabwera ndi Bar W, zina ndi Circle R, zina ndi Tripod. Izo ndi zoyikidwa chizindikiro ndi zizindikiro zosiyana, koma izo zonse ndi mtundu weniweni wa Herefords.” Ndiko kulondola.

¹⁶² Ndi momwe ziriri. Ife tikhoza kukhala tiri Amethodisti, Abaptisti, *ichi*, kapena *icho*, kapena *china*. Koma bola ngati iwe uli Mkristu wa mtundu weniweni, mwa mphamvu ya Mzimu Woyera, ndi chinthu chokha chimene chingakhoze kudza ku msipu, kulowa mu Kholalo. Chifukwa, “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi.” Ndipo ife timakhala anthu amodzi, Mpingo umodzi, tiri ndi lingaliro limodzi ndi cholinga chimodzi: kuti timupatse ulemero Yesu Khristu pamene ife tikadali pano pa dziko lapansi. Kumwamba kumodzi! Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo ife tiri othokoza kwambiri chifukwa cha izo.

¹⁶³ Tsopano ine ndadutsitsa nthawi yanga, ya kuyankhulana nanu, chifukwa inu muyenera kufulumira kuti mubwerere mu nthawi pang’ono yokha. Koma ndi angati amakonda kuyankhula kwa mtima ndi mtima? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukuoneka ngati. Inu mukumvetsa izo. Ife tikhoza kuyankhula maora pambuyo pa maora.

“Ndipo tsopano,” ngati mutanena kuti, “M’bale Branham, kodi inu mungazifotokoze izi kwa ine?” Ine sindingakhoze. Ine ndikukhumba ndikanamakhoza, koma ine sindingakhoze. Ndi zosatheka.

¹⁶⁴ Iwe sungakhoze kufotokoza zinthu zauzimu. Ndipo pamene iwe uyesera kuti uchite izo, izo ziri basi monga Iye anandiuizira ine, iwe umayambitsa kufanizitsa kwa chithupithupi kuti kuyambe. Mukuona? Iwe ukachita izo. Izo zikakhala zenizeni basi. Izo zimadzachita izo. Ndipo ndi—ndi cholepheretsa kwa Thupi la Khristu. Inu mukudziwa chomwe ine ndikutanthauza? Izo—izo—izo zimayambitsa makangano.

¹⁶⁵ Tsopano, chinthu choti nkuchita ndi kukhala woona mu mtima mwako, kumawakonda Ambuye ndi mtima wako wonse, ndi kungokhala wothokoza basi kuti Mulungu akuyendabe chamtsogolo nafe, Ambuye Yesu Khristu woukitsidwa.

¹⁶⁶ Ndipo ine ndikunena izi, ndi kupanga kuneneratu uku. Ine sindiri kunena izi mu Dzina la Ambuye, tsopano. Ine ndikuzinena izi, monga m’bale wanu. Ine ndikuneneratu izi. Ndipo mvetserani mwatcheru. Ine ndikuneneratu kuti Amereka, chaka chino, United States, chaka chino, mwina

alandira Khristu kapena iye ayamba kugwa, kuyambira chaka chino. Ndipo ino ndi nthawi ya Amereka kuti alape. Ndipo ngati iye satero. . . Ine ndinaneneratu izo pa, ine ndikuganiza, ndi pafupi Januwale pa 15 kapena pa 16 chaka chino, nkungomverera kutsogozedwa kuti ndizinene izo. Ndipo izo. . . Ine ndakakamirana ndi icho.

¹⁶⁷ Ndipo ine ndikuyang'ana pa magudumu akuzungulira. Ine ndazindikira mlaliki wamkulu, wotchuka, Billy Graham, iye wabwerera kuchokera kutsidya kwa nyanja ndipo iye anakonza misonkhano yake, ku New York ndi malo aakulu awa, kuti akhudze pachirikati pomwe pa mtsempha, ndi zina zotero. Ndipo ine ndikumuwona uyo, M'bale Roberts atathamangitsidwa ku dziko lakunja. Bambo Arganbright akundifuna ine, akatha Juni, ndi iwo, kuti tipite mu Germany, mpaka kukafika ku South Afrika ndi kudutsa uko, koma chinachake chikundigwirira ine ku Amereka. Ndipo ena onsewa akuwoneka kuti ali mwanjira yomweyo.

¹⁶⁸ Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Amereka alandira kuitana kwake kotsiriza, chaka chino. Kulondola. Ine ndiyenera kukhala wolimbantima. Ndikamayang'ana pa matepi awa pansi apa. Iwo akhoza kumadzaseweredwa zaka makumi awiri kuyambira lero. Mwaona? Iwe uyenera kusamalitsa zomwe iwe ukuzikamba, zisamalitsa zomwe iwe ukuzinena. Koma ine ndikukhulupirira izo. Tsopano, Ambuye sanandiuze ine izo. Koma ine ndikukhulupirira izo, kuti Amereka mwina amulandira Khristu kapena amukana Iye, kwathunthu, chaka chino. Ndipo ine ndikuneneratu kuti iwo amukana Iye. Ine ndikutero.

¹⁶⁹ Taonani zomwe iwo akuchita uko mu Florida, kwa Jack Coe. Taonani zomwe iwo akuchita, njira yonse. Angakhoze bwanji konse. . . Ndizo zosakhala mwamalamulo nkomwe, kumuchotsa munthu mu dziko. Ife tiri nawo ufulu wa kuyankhula. Ndithudi, ife tiri nawo. Koma iwo ama. . .

¹⁷⁰ Chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo ayesera kuti aziletse zonse izi. Iwo ayesera kuti asiye kupempherera odwala, ndi kuika chomangira pa izo. Ndipo ingokumbukirani kuti: pamene kuzunza kukuyamba, Mpingo, Iwo ukufika pamwamba Pake penipeni apo. Nthawizonse umakhala wopambana. Inde, bwana. Ndipo Mulungu akuchitira izo zonse palimodzi.

¹⁷¹ [M'bale ati, "Ameni. Ulemerero kwa Mulungu! Ameni. Ameni. Ameni. Ameni. Ndi ulemerero kwa Mulungu!"—Mkonzi.] Matamando akhale kwa Mulungu Yemwe amatipatsa ife chigonjetso! ["Ulemerero kwa Mulungu! Ulemerero kwa Mulungu!"]

¹⁷² [Alongo awiri akuyankhula mu malirime ena, pa nthawi imodzi.] Funafunani kutanthauzira tsopano, tiwone zomwe Iye amati anene kwa ife. [Alongo awirinso akuyankhula mu

malirime ena, pa nthawi imodzi. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . ndi kulondola.

¹⁷³ Pali kutanthauzira koti kutsatire izi tsopano. Aliyense molemekeza kwenikweni. Ndipo donayu wayankhula, yense yemwe iye anali. Mvetserani mwatcheru kwenikweni. Muwalole iwo amene amadziwa, tsopano, onani. [Mlongo akuyamba kuyankhula mu lirime lina—Mkonzi.] Shi-shi-shi-shi-shi! [Mlongoyo akupitirira kuyankhula mu lirime lina, pamene mlongo wina akupereka kutanthauzira, pa nthawi yomweyo.]

¹⁷⁴ Ndi mitu yanu yoweramitsidwa, inu mwamva kutanthauzira uko. Ndi angati muno akufuna kuti amulandire Khristu ngati Mpulumutsi waowao, kuti akumbukiridwe mu pemphero? Kodi inu mungakweze manja anu mokweza kwenikweni pakali pano, mmwamba momwe kuti ife tikhoze kumawona yemwe inu muli, mmwamba kwambiri.

¹⁷⁵ Tipeze kayimbidwe pang'ono pa limba, ngati inu mungatero, kwa mphindi pang'ono.

¹⁷⁶ Pamene inu mukuweramitsa mutu wanu tsopano, ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, pamene liwu lanena kuti izi zinali Choonadi. Ngati inu muli kubweramo konse, bwerani tsopano.

¹⁷⁷ Atate athu Akumwamba, ife tikupemphera kuti mu Dzina la Yesu Khristu, kuti, pamene Mzimu Wanu ukusunthira pa nyumba ino tsopano. Ndipo maliwu amveka ndipo anena kuti nthawi yake inali inoyi, oralo ndi lino. Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti, powona manja onse awo omwe anakwera mmwamba. Ena, akhoza kukhala manja makumi atatu kapena kupitirira, amene anakwera mu mlengalenga tsopano apa, kuti amulandire Khristu ngati Mpulumutsi waowao; akumvetsera Uthengawu, podziwa kuti ife tiri pa a nthawi yotsiriza.

¹⁷⁸ Moto wa chitsitsimutso uwu pa phiri lililonse. Mulungu analonjeza, mu masiku otsiriza, kuti Iye akanadzautsa zinthu izi, kuti azidzatsimikizira kuti Iye anali Mulungu, ndi pakati pathu ndipo akuchita izo zomwe zinali zolondola, ndi kumasonyeza zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa pakati pa anthu, kuti akhungu aziwona, ogontha azimva, ndipo pakhale pali mautumiki aakulu auzimu akuchitika. Ndipo lero, Ambuye, ife tikukhala moyo kuti tiziziwona izo.

¹⁷⁹ Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti aliyense wa ana osauka awa, omwe anakweza mmwamba manja awo tsopano pompa, kuti iwo amafuna kuti akulandireni Inu monga Mpulumutsi wawo, kuti Inu muwapulumutse iwo ku tchimo. Perekani izo, Ambuye.

¹⁸⁰ Ndipo ine ndikupemphera, naponso, kuti pamene ife tikanali mu kusuntha kwakukulu uku tsopano lino, kuti Mzimu Woyera udzaza mtima uliwonse, mwatsopano. Yatsani moto watsopano,

Ambuye, mu miyoyo yawo. Mulole iwo azituluka ali ndi changu, atatha kumva; mwamsanga pamene mawu aja anayankhulidwa, kuti fuko lathu lokonedwali likanati likane choperekedwacho.

¹⁸¹ O Mulungu, maufumu aakulu ayenera kuti agwe. Chinthu chachivundi chirichonse chiyenera kuti chipereke njira kwa chachisavundi, O Mulungu, pamene ife tikuziwona izi. Ife tikumaima uko pa mabwinja amakedzanja a Roma, kuwona pamene dziko lalikulu la mfumu yaikulu, tsiku lina linaima ngati malo ophukira a dziko, malo owalitsitsa mu dziko lonse. Ndipo, lero, iwe ungakumbe mapazi makumi awiri pansu pa nthaka, kuti ukapeze mabwinja a ufumu waukuluwo. Kutali, kumene nthawiyina kachisi anali, Usilamu wa Omar waimapo. Zinthu zambiri zazikulu, mafuko aakulu, Alexander the Great wotchuka, ndi Greece, ndi malo ena ambiri, momwe maufumuwo agwera!

¹⁸² Mulungu, ife tikuwona maziko a fuko lathu akuphwasuka, chifukwa cha kukana kwa Uthenga. Pamene amuna amphamvu asesa fuko lino, kupesa podutsa mu malo aliwonse, maulaliki a Uthenga amveka; mzimu wonga wa Yohane M'batizi, osati pochita zozizwitsa kapena kunena kalikonse kokhudza zozizwitsa, koma wasesa mu fuko lonse. Ndiye mphamvu yochita-zozizwitsa ya Yesu inatsatira izo, monga zinachitira ndi Yohane, ndipo panobe fuko lathu, mowa, fodya, malo a mowa a usiku, tchimo likuwunjikana ku mbali iliyonse. Chitukuko chatu chachikuluchi chikugwa, igwa. Chirichonse chiyenera kuti chipereke njira. Maufumu onse awa ayenera kuti agwe, kuti Ufumu wa Mulungu ulowetsedwemo mwa kuwala kwake, ndi Zakachikwi zazikulu zibwere mmalomo.

¹⁸³ Kuwuona mtengo wakale, umene nthawiyina, zaka zingapo zapitazo, ndiri mnyamata, unali; pamene unali waukulu, nthambi zachifumu, momwe ine ndinkaganizira kuti mtengowo ukanadzakhala pamenepo kwa mazana a zaka. Ndipo lero uli chitsa, podziwa kuti zinthu zachivundi zonse ziyenera kupereka njira.

¹⁸⁴ Ine, naponso, Ambuye, nthawiyina ndinali mnyamata, ndikudziwona ndekha ndikupereka njira tsopano, ndikufikira pamwamba pa chingwe kutsidya, kuwona kulowa kwa dzuwa. Lero, mitu yambiri ya imvi yaweramitsidwa mu nyumba ino, omwe nthawiyina anali amphamvu, anyamata okongola. Akazi ambiri omwe aweramitsa nkhope zawo, amakwinya, ndipo tsopano misonzi ikudula njira ya khwinya pa nkhope zawo zomwe nthawiyina zinali zokondeka ndi zokongola, ali asungwana. O Mulungu! “Mnofu uliwonse uli ngati udzu.” Mapeto ali pafupi.

¹⁸⁵ O Khristu wa Mulungu, alandireni anthu osauka awa alowe mu Ufumu Wanu. Tsiku lina, ine ndiyenera kudzaima Kutali pa—pa Mpando wachifumu wa Mulungu, ndi kudzayankhira

pa utumiki wanga, kudzayankhira pa zinthu izi zomwe Inu mwandiloleza kuti ine ndizizichita, Ambuye, pakati pa anthu, kuti ndiwonetsera chiukitsiro cha Ambuye Yesu. Mulungu, ine ndiyenera kudzayankhira pa izo. O Mulungu, muwotcherere changu pansu pa mtima wanga, mochuluka chuluka, ndi nzeru, kuti ndizidziwa momwe ine ndingatidziwatsogolerera anthu kwa Ambuye Yesu.

¹⁸⁶ Lero, Atate, Inu mwalonjeza mu Mawu Anu Oyera, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wachoka ku imfa kupita ku Moyo.”

¹⁸⁷ Manja ambiri kudutsa muno anapita mmwamba, Ambuye. Anthu ambiri osauka, otaika, ambiri a iwo obwerera mmbuyo ndi ochoka mu njira. Mulungu, perekani izo, miniti yomwe ino, imene Mzimu Woyera ukuperekerera umboni kuti zinthu izi ndi zooni, kuti ife tiri pamapeto a nthawi, ndipo iwo akuzindikira kuti tsiku lina izo ziyenera kudzachitika. Mulole iwo amulandire Khristu pakali pano, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

¹⁸⁸ Kodi alipo winawake muno tsopano, omwe sanakweze konse manja awo pa kuitana koyamba? Kodi inu mungakweze dzanja lanu tsopano? Ndi kuti, “Ine ndikufuna kuti ndimulandire Khristu, pa nthawi ino, ngati Mpulumutsi wanga.” Kodi inu mungachite izo? Wina wakenso? Yemwe sanateropo . . .

¹⁸⁹ Kodi inu munazindikira momwe Moto unakhudzira nyumbayi pamene Mawu aja anapitapo? Mukuona? Ine ndikukhulupirira, mzanga. Mulungu akudalitseni inu, bwenzi wanga wamng’ono, mnyamata uli ndi dzanja lako mmwamba. Mulungu, akupatse m’bale wanga. Iwe uli nawo Moyo Wamuyaya pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu.

Ine ndikudabwa, mu khonde kwinakwakeko?

¹⁹⁰ Ngati ife tikuwona kuti Mulungu anazilonjeza zinthu izi, ife tiri pano kuti tiziwone izo zikufika pochitika. Ife tikudziwa kuti Mulungu analonjeza izo. Ndipo chirichonse chimene Mulungu alonjeza, Mulungu ali wokakamizidwa kuti azichite izo.

¹⁹¹ Kodi angakhalepo wina? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndikuliwona dzanja lanu. Kodi winawakenso angakweze dzanja lake? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndikuliwona dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Ine ndikuliwona dzanja lako. Wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndikuliwona dzanja lanu.

¹⁹² Winawake mu khonde. Ine ndikufuna kuti ndimuwone winawake, mmwamba umo mu khonde, yemwe sali Mkhristu, akufuna kuti anene. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndimangodziwa kuti iwe unali mmwamba umo, mwananga. Alipo winawake, chifukwa Mzimu Woyera ukuwoneka kuti ukunditsogolera ine ku khondelo. Ine sindikudziwa chifukwa

chake. Ine si wotentheka. Ngati ine ndiri, ine sindikutanthauza kuti ndikhale. Koma basi zimangowoneka ngati kunali winawake mu khondelo. Mulungu akudalitse iwe, mwananga. Mulole inu. . . Ndipo ngati uyo ali mkazi wako pafupi nawe, mutamakamutumikira Ambuye Yesu ndi mtima wanu wonse. Mulole Izo zikasinthe moyo wanu, kwanu. Izo zikatero. Iwe utakakhala wantchito Wake.

¹⁹³ Kodi alipo winawake, basi tisanati titseke tsopano, ine ndisanati ndipereke msonkhanowu kwa M'bale Boze? Anyamata ayenera kuti abwere muno, mu maminiti pang'ono, ndi kudzayamba kupereka makadi apemphero. Mungatero inu, basi dzanja limodzi lina, kwezani dzanja lanu, penapake mu nyumbayi? M'bale Joseph. . . Ngati inu muti mungokweza dzanja lanu, mphindi yokha; ine ndikufuna kuti ndipemphere ndi inu, kachiwiri. Inde. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikukuonani inu mmusi umo. Zikomo inu, bwana wachifundo. Mulungu akudalitseni inu uko, mnyamata. Izo nzabwino kwambiri.

¹⁹⁴ Tsopano, izi zikhoza kumawoneka mwachilendo pang'ono kwa ena a inu, momwe mawu amodzi aja akanakhoza kuswa chinachake monga choncho, ndipo Moto nkumwazikana. Mwaona? Ndi chifukwa chakuti ndi Choonadi, ndi—mau otsegulira kwa Uthenga, inu mukuona, kuti ife tiri pa mapeto a nthawi.

¹⁹⁵ Mulungu akudalitseni inu, bwana. Ine ndikuliwona dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu.

¹⁹⁶ Tsopano, ine ndikukuuzani inu, abwenzi, alipo ambiri omwe akhala muno, ine ndikukhulupirira, omwe ati adzapirire kuzunzika kowopsya chifukwa cha chikhulupiriro chawo izo zisanati zisindikizidwe nkutha.


¹⁹⁷ Mulungu akudalitseni inu. Winawakenso akweze dzanja lake? Mulungu akudalitseni inu, kutali komwe mmbuyomo. Ine ndikuliwona dzanja lanu, bwana. Wina wakenso? Tsopano, wina wakenso, kwezani dzanja lanu mofulumira ndithu. Pamene ife tikuyembekezera pemphero lobalalitsa, ngati inu muti mukweze dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, mwanawanga. Mulungu akudalitse iwe, mwananga. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikuliwona dzanja lanu, pamwamba pa mwamuna uyo. Inde. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Ine ndikuliwona.

¹⁹⁸ Izo nzodabwitsa; kungomulandira Khristu. Inu, pamene inu mukukweza dzanja lanu, Mulungu akulemba izo pa Bukhu la Moyo. Miniti yomweyo pamene inu mukukhulupirira, inu mukudutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, pamene inu mukukweza dzanja lanu. Kodi inu munakweza motani dzanja lanu? "Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine kupatula Atate Anga akamukoka iye, poyamba." Ndi zimenezo. Mulungu, pano, akukoka; inu mukukweza dzanja lanu. Angelo akulemba dzina

lanu pa Bukhu la Moyo. Izo zikukhazikitsa izo. Tsopano inu mulandira Mzimu Woyera ngati inu muti mungokhulupirira.

Tsopano, ndi mitu yathu yoweramitsidwa kachiwiri.

¹⁹⁹ Atate athu Akumwamba, tumizani madalitso Anu. Ndipo ine ndikukuthokozani Inu, Atate, chifukwa cha khamu lalikulu ili la anthu lomwe likungolandira kumene Khristu. Ine ndikukuthokozani Inu chifukwa chowutsimikiziranso Uthenga Wanu, Ambuye, ndi kuwupereka Iwo, ndi kuchita zinthu zomwe Inu mwatichitira ife lero. Anthu awa akhale ali okondwa masiku onse a moyo awo. Inu mwawapatsa iwo Moyo wosatha, pakali pano, chifukwa iwo akhulupirira pa Ambuye Yesu. Ndipo, Atate, pamene kuitanira paguwa uko kuti kupangidwe, mu mphindi chabe, kuti abwere kuno ndipo mwawokha kudzaima mozungulira guwali kapena mu mpita, kwinakwake, ndi kumapemphera kwa Inu, ndi kumapereka mathokozi chifukwa cha chipulumutso chawo, ine ndikupemphera kuti dzanja lirilonse lomwe linakwezedwa iwo adzaima mu mpitawu, penapake, ndi kumapemphera kwa Inu, ndi kupereka mathokozi chifukwa cha kuwalandira iwo, kapena kuwalandira iwo alowe mu Ufumu Wanu. Perekani izo, Ambuye. Mulole madalitso Anu Amuyaya akhale ali pa iwo.

²⁰⁰ Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa, M'bale Joseph azipitiriza nalo, pemphero. 

KODI MASOMPHENYA NDI CHIANI? CHA56-0408A
(What Is A Vision?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Epulo 8, 1956, ku Lane Tech High School mu Chicago, Illinois, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2002 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2012 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org